

ALI KUTI IYE, MFUMU YA AYUDA?

 Ndipo ine ndithudi ndikuyamikira zimenezo. Imeneyo ndi mphatso yanga yoyamba ya Khristimasi, chotero ine ndinali woyamikira kwambiri. Ndipo, chabwino, ngati ine nditangolalikira tsopano popanda kuyesera kuti ndiyitsegule iyo! Ine ndimakhala ngati mwana ndi ziyembekezera za Khristimasi zimenezo, a—kuyembekezera chinachake, inu mukudziwa, iwe umangomverera kuti pali kodzidzimutsa kakang’ono ndipo ukungoyenera kuti ukafikire iko. Ndipo, inu mukudziwa, pamene ngakhale pamene ife titakalamba, ine sindikuganiza kuti ife timataya umwana wathu wonse. Kodi inu mukuganiza chomwecho? Ndife ana akulu basi. Ndizo za zimenezo.

² Chabwino, Ambuye alemekezeke! Ndife okondwa kukhala tiri kunja kuno kachiwiri, pa mmawa wabwino wachisangalalo uno, ndikuyembekezera madalitso a Ambuye kuti apitirire ndi ife pamene ife tikupitirira mu msonkhano, monga ine ndikutsimikiza kuti Iye watero.

³ Ine ndikuganiza, mmawa uno, iwo akhala ndi mphatso zina za ana. Kapena—kapena ndi... [M’bale Neville akuti, “Atenga kale izo.”—Mkonzi]. Zatengedwa kale, mphatso za ana. Chabwino, izo ndi zabwino kwambiri.

⁴ Tsopano, ndikungofuna kuti ndipereke lipoti laling’ono pa msonkhano wathu wotsiriza, ngati ziri zabwino, ndipo pa nthawi ino. [M’bale Neville akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Inu anthu ndinu amene mumapemphera ndipo mumagwiritsitsa kwa Mulungu, kuti ine ndipite kunja mmisonkhano imeneyi. Ndipo ine ndikungofuna kuti ndingopereka kuwomba nkota pang’ono kwa—kwa misonkhano yotsiriza basi.

⁵ Chimodzi cha zochitika zopambana za msonkhano wotsiriza, chinali mu... chinachitika mu Shawano, Wisconsin. Kunali ku nyumba yoyankhuliramo ya high school, nyumba yolankhuliramo ya high school yatsopano, pamene tinangotsala pang’ono kukonzekera kuti tiwapempherere odwala. Ine ndinali nditangopanga kuitanira paguwa, ndipo ambiri anali atakweza manja awo, kuti amulandire Khristu ngati Mpulumutsi wawo wawo. Ndiyenyo zinali pamenepo pamene ine ndinazindikira chinachake chikuchitika, chimene chinali mwa omvetsera kumene, kachidutswa kakang’ono kuchokera kwa ine. Ndipo anali mwamuna wa pafupifupi usinkhu wa zaka sevente kapena sevente-faivi zakubadwa. Iye anagwa nkufa, anafa ndi nthenda

ya mtima. Thovu linatuluka kuchokera mkamwa mwake, ndipo madzi anamwazikira pa zovala zake. Ndipo—ndipo mkazi wake, mosimidwa kwenikweni, akusisita nkhope yake.

⁶ Ndipo—ndipo ine ndinadziwa kuti imeneyo inali ndale ya mdani. Iye amachita zinthu zimenezo kuti angowabalalitsa anthuwo, mwaona, ndiyeno, pamene iye achita zimenezo, izo zimapita kwa wasokonezeka. Izo zachitikapo nthawi zambiri mu msonkhano. Posakhalitsapa mu New England izo zinachitika monga chomwecho kachiwiri, basi kusanachitike kuitana kumeneko.

⁷ Ndipo chotero kuti anthuwo asakhale otengeka, ine... Mu nthawi za mtundu umenewo, iwe umayenera kusunga nzeru zako, kuti uwone chimene Mzimu Woyera unganene. Chifukwa, ife timaphunzitsidwa mu Malemba, kuti, “Zinthu zonse zimachitira ubwino kwa iwo amene amamukonda Mulungu.”

⁸ Ndipo panali ambiri a ana a Mulungu, omukonda Iye. Ndipo ine ndinakhala ndikumuyang’anitsitsa munthuyo, ndipo powona kuti iye anali atachita thovu m’kamwa. Ndipo... Ndipo monga aliyense akudziwira, pamene imfa imukantha munthu, kawirikawiri madzi amachokamo, inu mwaona. Ndipo iwo... Ndipo mkazi wake, akusisita nkhope yake, ndipo iye amangopita monga *choncho*. Kutu anthu asamuzindikire iye, Ine ndinati, “Amuna anu, kodi inu mungafune winawake kuti awatengere iwo madzi akumwa?” kuti akhale ndi chidwi.

⁹ Ndipo iye anati, “M’bale Branham, ine ndikungozisiya izo zonse kwa inu.” Ndipo iye anali wa—wa Chilutera, chipembedzo chake.

¹⁰ Ndipo kenako ndinaganiza kuti ndiyitanire mzere wa pemphero, ndi kuwabweretsa anthuwo, kuti ndiwapempherere iwo. Koma, mmalo mochita zimenezo, Mzimu Woyera unayamba kuyenda kupita mu msonkhano, pa anthu, nkumangowaitana iwo. Ndipo Iwo unamudutsa bambo wachikulireyo, pafupifupi kawiri. Ndiyeno, zonse mwadzidzidzi, ine ndinati, “Ife tingopemphera.”

¹¹ Ndipo pamene ine ndinayamba kupemphera, ine ndinadzimva ndekha ndikupemphera, chimene chinanena kwa imfa iyi, “Mmasule iye.” Ndipo sizinaposerenso momwe izo zinanenedwera, mwakuti, munthuyo anakhalanso ndi moyo, ndipo anaimirira pa mapazi ake. Ndipo mzinda wonsewo unanjenjemera nazo izo, zomwe Yehova anali atachita.

¹² Ndiyeno, ndithudi, pa misonkhano inayo. Ndipo vuto limodzi laling’ono ine ndikungofuna kuti ndibwereze, osati kuti nditenge yochuluka kwambiri ya nthawi yanu, koma kunali ku Los Angeles posachedwapa. Ine ndinali kukhala ndi M’bale Arganbright.

¹³ Ndipo ambiri a inu mukudziwa momwe izo zimakhalira mmalo, anthu akuitana. Kumakhala anthu amene amakhala

osowa. Ife sitimawaweruza anthu chifukwa chomaimba ndi kufuna pemphero. Imeneyo ndi ntchito yathu, ndi kuwapempherera anthu amenewo.

Ndipo izo zinali zoipa basi pamenepo, chifukwa ife tinali nazo zinthu zambiri zazikulu zimene Ambuye Mulungu anali atachita. Ndipo, mmodzi, panali munthu wolumala, anakhala wolumala zaka twente chakuti, ndipo ankagona pa machira ake. Ndipo Ambuye Mulungu anamuchiza munthuyo, ndipo iye anabwera akuyenda kuchokera ku msonkhano. Ndipo izo zinayambitsa kukondoweza pang'ono pakati pa mipingo.

¹⁴ Ndiye, mmawa wina, ine ndinamva foni ikuyitana. Ndipo M'bale Arganbright, kumene ine ndimakhalako, anali basi asanabwere pa nthawi imeneyo, kuti ayankhe foniyo. Ndipo ine ndinanyamula foniyo ndipo ndinaiyankha iyo, ndipo uyo anali a—wamishonare wamng'ono wa chi Mexico. Ndipo iye anati, “Ine sindimadziwa kuti—kuti muli mu mzindawu, M'bale Branham.” Iye anati, “Ine—ine—ine ndikudziwa kuti inu mukhala ndi msonkhano usikuuno, kumusi kwinakwake cha ku Cow Palace.” Ndipo iye anati, “Ine ndiri ndi mnyamata wamng'ono amene sanakwane miyezi faivi.” Ndipo anati, “Iye akufa, ndi khansa.” Ndipo anati, “Ine ndikudziwa si mwambo wake kuti ndichite izi, koma,” anati, “kodi pangakhale chifundo chopezeka, kuti inu mubwere ndi kudzamupempherera mwanayo?” Taganizani, bwanji ngati ameneyo akanakhala mwana wanu?

¹⁵ Ndipo ine—ine ndinati, “Ine ndikuwabweretsa Bambo Arganbright pa foniyo, ndipo inu mungondiuza ine, mulole... muwalondolere iwo kumene kuli chipatalacho, chifukwa ine sindikuwudziwa bwino mzinda umenewu.” Mamailosi masikweya foro handiredi a mzinda; ine sindikanachipeza chipatalacho.

Bambo Arganbright anabwera. Iye anati, “M'bale Branham, inu...”

Ine ndinati, “Ine ndikumverera motsimikiza kutsogozedwa kuti ichi ndi cha Mzimu Woyera.”

¹⁶ Chotero ife tinapita ku mzindawo, ndipo kumeneko ku chipatala. Ndipo m'bale wa Chimeico, ngakhale iye sanali woderapo, osati woderapo kundiposa ine, ndi bambo mwinamwake wa usinkhu wanga. Ndipo mkazi wake anali mkazi wachi Finnish, dona wamng'ono wa bulondi, dona wokondeka kwambiri. Ndipo iye anali njonda. Ndipo ife tinalowa mchipatalacho.

¹⁷ Ndipo, oh, ine ndimawona mawonekedwe ambiri, ife tonse timachita zimenezo, amene amatisokoneza ife ndi kubweretsa kutengeka kwathu, koma awo anali amodzi oyipisitsa amene ine ndinayamba ndawawonapo. Iwo anachita kumubweretsa mwana wamng'onoyo ku... pafupi ndi chipinda cha namwino,

ndi namwino wapadera. Ndipo, pamene ine ndinayang'ana, khansa inali itafalikira mu nsagwada zake zazing'ono, mpaka patali, iwo anachita kuika chiguduli kuzungulira mutu wake, kuwopera kuti mutu wake usaphulike nkutseguka. Ndipo mu nsagwada zake zazing'ono, momwe adotolo anayesera kuti adule khansayo, ndipo anapanga maenje aakulu, mmbuyo ndi mtsogolo, monga *chonchi*, njira yonse kuzungulira khosi lake laling'ono. Ndipo izo *zinangokulitsa* khansayo, ndipo ine ndizitchula izo mawu amenewo, amene “kufalikira” izo, angakhale mawuwo olondola. Ndipo iyo inapita mu lirime lake laling'ono, ndi kamwa ya mwana wamng'ono, osati kupitirira kutambalala *chomwecho*, lirime laling'onolo linali litatupa ndipo limathamangira kutalika *chomwecho*, ndipo linasanduka lakuda, ndipo chimene zimatseka mpweya kumene iye ankapumira pansi kuchokera mmphuno mwake.

¹⁸ Ndipo bambo ameneyo anayenda mozungulira, mmbali ya mwana wamng'ono uyu, ndipo anati, “Moni, Ricky.” Anati, “Mnyamata wamng'ono wa Adadi! Adadi amubweretsa M'bale Branham kuti akupempherere iwe, Ricky.” Ndipo mwanayo anawazindikira abambo ake.

¹⁹ Ndipo—ndipo iko sikamapumira nkomwe pamwamba *apa*, kotero iwo anachita kudula bowo pa mmero wake. Panali kakang'ono, kankangowoneka ngati kawezulo kakang'ono kozungulira komwe tinkakhala nako zaka zapitazo, kanali pa mmero wake wawung'ono. Ndipo iye ankapuma mpweya wake kudzera mu wezulo imeneyo. Ndipo namwino ankayenera kukhala pamenepo nthawi zonse chifukwa khansayo, imayamwa, imakhoza...imatseka kabowo kakang'ono aka. Ndipo iye amayenera kuti azikokera izo panja, monga *choncho*, izidutsiramo khansa kuchokera ku khansa. Ndipo manja ake aang'ono anali mu zingwe, kuchitira kuti iye asamakhoze kugwira *izi* ndi manja ake, kumakoka izo pamene iye akudzipotokola. Ndipo namwino amakhala pamenepo nthawi zonse. Pamene iye ayamba kudzipotokola, iye amakhoza kufikira pamenepo, kutenga zinthuzo ndi kusolola zinthu za khansa kuzitulutsa mu wezulo yake yaing'onoyo pamenepo pamene izo zimatulukira kudzera kummero kwake.

²⁰ Ndipo manja ake aang'ono, monga *chonchi*, akuwafikira abambo ake, mutu wake wawung'ono mmbuyo. Ndipo ake aang'ono...Chabwino, ndife abale ndi alongo. Thewera lake laling'ono, ilo silinali...Mwana wamng'onoyo, pamodzi, sizinali kutalika *chomwecho*. Sanali ndi miyezi faivi apabe, ndipo kanthu kakang'ono ako kanawazindikira abambo ake! Ndipo iye anati, “Ricky, mnyamata wamng'ono wa adadi!” Oh, momwe, zinasungunulira mtima wa munthu wa chitsulo. Ndipo iye anali akuyesetsa kuti azisewera naye iye, kapena kumamusisita iye, monga *chonchi*.

²¹ Ndipo ine, nditaima pamenepo, ine ndinaganiza, “Ambuye

Yesu, ngati Inu muli Kasupe wa chisoni chonse, ndipo chifundo chonse chiri mwa Inu, kodi Inu mungakhale ndi chisangalalo pomuwona wokondedwa wamng'ono uyu wagona apa, akufa monga choncho? Ine sindingakhoze basi kukhulupirira, ndipo sindidzakhulupirira konse, kuti ndicho—kuti ndicho chifuniro cha Mulungu Wamphamvuzonse, kuti aziwona zonga zimenezo.” Ine ndinaganiza, “Ndinu Kasupe wa chifundo. Ndipo ngati Inu muli Kasupe wa chifundo, ndiye Inu mungakhoze bwanji, Inu mungakhoze kukhala Mulungu wachifundo ndi kumasangalala kuwona chinachake chonga icho?” Ndinaganiza, “Kodi Inu mukanachita chiyani ngati Inu mukanaima pano?”

²² Chabwino, ine ndikuyembekeza kuti gulu langa lomwe laling'ono pano likundidziwa ine bwino mokwanira, kudziwa kuti ngati ine ndiri wotentheka ine sindikudziwa zimenezo. Ngati chirichonse chimene ine ndikufuna kuti ndikhale, ndi kuwonamtima. Pamene ndizidzakumana ndi Mulungu, ine ndikufuna ndidzacomane naye Iye ndi mtima woona, ndipo ine ndachita zopambana zimene ine ndikudziwa kuchita kwake.

²³ Koma Chinachake chinayankhula kwa ine pamene ine ndinati, “Ambuye, kodi Inu mukanachita chiyani ngati Inu mukanaima pano?” Chinachake chinayankhula moyankha, chinati, “Ine ndikuyembekezera kuwona chimene iwe uti uchite.”

²⁴ Ndipo pamene ine ndinayang'ana pa kanthu kakang'ano ako, ine ndinatenga dzanja lake laling'ono la kakhanda, osati lotambalala *chomwecho*, ndi kuliyika ilo mu zala zanga, monga *chonchi*, ndipo ndinaligwira ilo. Ndipo ine ndinati, “Mwa chikhulupiriro mwa Mulungu, ine ndikuika pakati pa khansa iyi ndi mwanayo, Magazi a Ambuye Yesu Khristu,” ndipo ndinangotembenuka ndi kuchokapo. Abambowo anatuluka nane limodzi. Ine sindikanakhoza basi kuyankhula zinanso.

²⁵ Ndipo ine ndinafika ku galimoto, ndipo iye anati, “M'bale Branham, apa pali zakhumi pang'ono zomwe ine ndakhala ndikukusungirani inu.”

²⁶ Ine ndinati, “Oh, m'bale wachifundo, musachite zimenezo.” Ine ndinati, “Ayi. Ine sindimatenga ndalama.”

²⁷ Anati, “Koma ichi ndi chachikhumi chimene chimapita ku utumiki.” Anati, “Ine ndimachisunga icho, kumaganiza kuti ndidzakuwonani inu tsiku lina.”

²⁸ Ine ndinati, “Kaziyikeni izo pa bilo ya Ricky wamng'ono uko.” Ine ndinati, “Iye, iye akazisowa zimenezo.” Ndipo chotero ine ndinapitirira mpaka ku nyumba.

²⁹ Ndipo mkati mwa maora awiri kuyambira nthawi imeneyo, nsagwada zazing'onozo zinali zitabwereranso, mwachibadwa, lirime linabwereranso pansu mkamwa mwake. Chifundo chachikondi, cha Atate wokoma mtima ndi wachikondi anachiwona kuti ndi choyenera kumuchiritsa mwanayo.

Mmawa wotsatira, mwanayo anali woti atumizidwa kwawo, mwana wabwino bwino.

³⁰ Ndipo pamene ine ndinali kukonzekera kuti ndizinyamuka...Ndithudi, izo zinafalikira Gombe la Kumadzuloko. Ndipo apa dokotala wina wotchuka anali atatumiza mdzukululu wake kuseri kwa Pasadena, ndipo anayika rodibuloko kumeneko, kuti ndikamupempherere mwana ameneyo; kumene iye anali atamubaya iye katemera wa penisilini, zinapangitsa khansa kuti ibwere ku mbali yake, mwana wamng'ono kwambiri, pafupifupi ziwiri.

³¹ Ndipo chotero wamishonare wamng'ono uyu, wa Chimexico anaimba, ndipo iye anati, "Ine—ine ndiyenera ndimuwone M'bale Branham ine ndisanachoke." Ndipo mkazanga ndi ine tinali kale mgalimoto.

³² Ndipo ine ndinali nditagwira nsomba, zaka zingapo zapitazo, kumeneko ku Mtsinje wa No Return, ndi Amuna Azamalonda Achikhristu. Walt Disney, gulu lija kunja uko, anali nazo izo, woyendetsa takisi, chifukwa ndi kotchuka pa dziko lonse, chifukwa cha mphuta za utawaleza. Ndipo ine ndinali kuyikonza iyo mgalimoto.

³³ Ndipo uko kunali a—galimoto yaing'ono imapita kumeneko, kumbuyo, ndipo analumphira bambo wamng'ono uyu, wachi Mexico. Ndipo misonzi ikutsikira pansi mmasaya ake, pamene iye amathamanga ndipo anadzavula chipewa chake; ndi mkazi wake wamng'ono wachi Finnish. Ndipo iye anati, "M'bale Branham, pano pali zakhumi zomwe Ambuye atatumiza kwa inu."

"Oh," ine ndinati, "m'bale!"

Anati, "Inu mukudziwa, Ricky akupita kunyumba lero."

³⁴ Ndipo ine ndinati, "Ndine woyamikira chifukwa cha zimenezo." Iye...Ine ndinati, "Koma ine ndinakuuzani inu kuti mutenge—zakhumi ndi—ndipo mukaziike izo pa bilo ya Ricky."

³⁵ Iye anati, "Ndizo basi zimene ine ndimati ndikuuzeni inu, M'bale Branham." Iye anati, "Pamene ine ndinapita kuti ndikamulipire dokotalayo, mmawa uno, ine ndinayika izi, ndalama izi pa iye. Ine ndinati, 'Dokotala, ine ndikufuna kuti ndikulipireni zina pa bilo.' Iye anati, 'Bambo, musatchule nkomwe izo kwa ine. Inu mulibe nane ngongole.' Iye anati, 'Ndicho chinthu chachikulu kwambiri chimene ndinayamba ndachiwonapo chikuchitidwa mmoyo wanga wonse.' Iye anati, 'Ndicho chopambana cha zopambana!' Anati, 'Inu mulibe nane ngongole.'"

³⁶ Izo zikungowonetsera kuti Mulungu wamoyo akadali moyo. Ndipo tsopano ife tisanatsegule Ake...Oh, pali zinthu zina zambiri zinachitika. Ine ndikukhumba ndikanakhala nayo nthawi yoti ndikuuzeni inu, koma nthawi siilola zimenezo.

³⁷ Ndipo tsopano, kuyambira koyambirira kwa chaka, Januwale, ine ndikuchokapo kupita kutsidya kwa nyanja kachiwiri. Pakuti . . . ine ndikakhala ndiri ku Kingston, Jamaica, ku—ku mabwalo a mjaha, mu Januwale, ndipo kuchokera kumeneko ku Puerto Rico, ndi kwina kotero.

³⁸ Chotero tiyeni ife tiweramitse mitu yathu kamphindi chabe, mu pemphero, kwa wamkulu wathu, wokondedwa Khristu.

³⁹ O Ambuye, Inu mwakhala pothawirapo pathu mu kam’badwo kalikonse. Ndinu thandizo lopezekeratu mu nthawi ya vuto. Ndipo kudziwa kuti Kukhalapo Kwanu kokonda sikudzalephera konse, Iko kumapita patsogolo pathu. Ndipo ife timaphunzitsidwa kuti Angelo a Mulungu amawazinga iwo amene amamuwopa Iye.

⁴⁰ Bweretsani pa ife, lero, Ambuye, mantha aumulungu amenewo, kuti ife tikhoze kudziwa kuti ndife omvera a dzanja Lanu, ndipo tidzaima tsiku lina mu chiweruzo Chanu Chaumulungu. Ndipo alipo mankhwala amodzi okha amene ife tikuwadziwa, ndipo amene Mawu Anu amawaphunzitsa, ndiwo Magazi a Mwana Wanu Yesu, amene akutipangira ife chitetezero, mmawa uno, mu Kukhalapo kwa Wamphamvuzonse, kutibweretsa ife mu chiyanjanitso kwa Iye, kupyolera mu zoyenereza Zake. Ndiyeno izo zaperekedwa kwa ife, chisomo chosatiyenera, ndipo ife timamukonda Iye chifukwa cha izi. Ndipo pamene ife . . .

⁴¹ Mmalingaliro athu muli ma handiredi a zinthu zazikulu zimene Inu mwachita. Ndipo chachikulu cha zonsezo, ife tikhoza kuganiza za, ndi pamene Inu munatipulumutsa ife kuchokera ku moyo wa imfa, mmene mwa ife munkakhala imfa chifukwa cha tchimo ndi zolakwa. Koma pa kuvomereza chikhululukiro Chake, molingana ndi Mawu Ake . . . Pakuti kunalembedwa, “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wachisavundi.” Ndipo ife timawakhulupirira Iwo, ndipo tawavomereza Iwo, ndipo tikuchitira umboni Kukhalapo kwa Mzimu Woyera.

⁴² Ndipo tsopano mu choyipa chotsiriza ichi, maora otsiriza a mbiriyakale ya dziko lino, ndife oyamikira kwa Inu, O Mulungu, kudziwa zimenezo; pamene pali chisokonezo chochuluka cha malingaliro, “Ndipo anthu akuthamangira uku ndi uko,” monga Inu munanena kupyolera mwa aneneri oyera, kuti, mu tsiku lino, “idzafika nthawi imene anthu azidzapita kuchokera Kummawa, kuchokera Kumadzulo, Kumpoto, ndi Kummwera, kufunafuna kuti amve Mawu owona a Mulungu.” Ndipo ife takhala moyo kuti tidzaiwone nthawi imeneyo.

⁴³ Ndipo Inu munaneneratu kuti idzakhalapo nthawi, kuyambira pa kupachikidwa Kwanu mpaka Kudza Kwanu, “Tsiku limene silidzakhala usiku kapena masana. Ilo lidzakhala lachimbuzi, nthawi yolunda,” Kuwala kokwanira basi kuti

uwone momwe ungayendere. Koma Inu munati, “Mu nthawi ya kumadzulo, kudzakhala Kuwala,” Mwana yemweyo, Khristu yemweyo, amene anawuka powonekera Kummawa. Ndipo mogwirizana ndi malo, dzuwa likudutsa mbali yopingasa ya dziko lapansi, ndipo tsopano likukalowa Kumadzulo, koma ndi dzuwa lomwelo limene linatuluka Kummawa. Chomwechonso Mwana wa Mulungu yemweyo akutumiza Mzimu Wake mmasiku otsiriza ano, kuti akasonyeze kuti Malemba Ake sangathe kusweka, Limodzi lililonse liyenera kukwaniritsidwa.

⁴⁴ Pa kulowa kwa Khrisimasi yopambana iyi, pamene, ife tikudziwa pang’ono koma iyi ikhoza kukhala yomaliza mwa izi zomwe tidzakhalepo limodzi. Ndipo ife tikupempha kuti Mwana wa Mulungu wamoyo akhale pakati pathu mmawa uno, ndipo adzayankhule kwa ife kukomamtima Kwake ndi chifundo Chake, ndi kupereka kwa ife kukhululukira kwa machimo athu.

⁴⁵ Ndipo ife sitikuwaiwala, Ambuye, iwo amene ali osautsika ndi osowa kukhudza Kwanu kwa machiritso, Mulungu yemweyo Amene anamulola Ricky wamng’ono kuti akhale moyo, anawabweretsanso akufa, monga Inu munalonjezera kuti Inu mudzachita mu tsiku lotsiriza. Ndipo Mawu Anu ndi owona. Ife tikukhulupirira kuti Inu muli pano mmawa uno, wopezeka ponseponse, ndipo wofunitsitsa kuchita zochulukira kwambiri, kuposa zonse zomwe tingapemphe kapena kuziganizira. Ife tikuyembekezera pa Inu, Atate, mu Dzina la Ambuye Yesu, Mwana Wanu. Amen.

⁴⁶ Tsopano, usikuuno, ngati Ambuye alola, ine ndikufuna kuti ndidzakhale ndi msonkhano waulaliki. Sindikudziwa basi penipenipo mpaka pano pamene Uthenga wanga uti udzakhale, monga m’busa wathu wachisomo ndi wokondedwa wandipempha ine kuti ndikhale ndi misonkhano iwiri lero. Ndipo ine ndiyesetsa zimenezo, mwa chisomo cha Mulungu. Ndipo ine ndikufuna kuti ndiyankhule pa Mesiya wakudza, kapena chinachake cha nkhani imeneyo, kwa usikuuno, kapena dongosolo limenelo.

⁴⁷ Mmawa uno, pokhala kuti inali Chi-...Lamlungu basi isanafike Khrisimasi, ine ndikufuna kuti ndiyankhule pa chinachake chimene ine ndikukhulupirira ang’onowa, amene angobalalitsidwa kumene ndipo atenga malo awo mu mpingo, akhoza kumvetsetsa; chaching’ono, chomwe ife tingachitche, mutu wa Khrisimasi.

⁴⁸ Ndipo inu amene mukukhumba kuti mutembenezire mu Malemba opatulika, mungatembenezire ndi ine ku Uthenga wa Mateyu Woyera, mutu wa 2, pamene tikuwerenga Mawu Ake.

⁴⁹ Ndipo musayiwale, misonkhano iyamba pa hafu pasiti seveni. Nkulondola uko, sichoncho izo, m’bale? [M’bale Neville akuti, “Hafu pasiti seveni. Inde.”—Mkonzi]. Hafu pasiti seveni,

ndendende, usikuuno. Ndipo udzakhala pafupifupi utumiki wa ora limodzi, utumiki wolalikira.

⁵⁰ Ndipo tsopano inu amene muli ndi Mabaibulo anu otsegula, ine ndikungofuna kuti ndiwerenge ndime kapena ziwiri kuchokera apa, kwa—mutu, ndipo tikupemphera kuti Mulungu atipatse ife nkhanayi.

Tsopano pamene Yesu anabadwa mu Betelehemu wa Yudeya mwa a mfumu...mmasiku a Herodi mfumu, taonani, apo panabwera amuna anzeru ochokera kummawa ku Yerusalemu.

Akuti, Ali kuti iye amene wabadwa ali Mfumu ya Ayuda? pakuti ife taiwona nyenyezi yake kummawa, ndipo tabwera kuti tidzampembedze iye.

⁵¹ Iwo ayenera kuti anali atatopa kwambiri. Inu mukuona, a—choti achitecho chinali chamsangamsanga. Ndipo iko kunali kulamula kwa mfumu, chotero izo zimayenera kuti zichitike. Ndipo izo zingawoneke zachirendo, kuti chochitika chachikulu choterocho monga ife tikuyang'anapo, Khristimasi yoyambirira, kuti lamulo loterolo linadzaperekedwa pa nthawi imeneyo. Koma, inu mukudziwa, Mulungu wa Kumwamba anakonzeratu zinthu zonse, kudzera mwa Yesu Khristu, ndipo kuti chirichonse chienera kugwira ntchito molingana ndi chifuniro Chake chachikulu. Ndipo pamene iwo anaima pamenepo, basi kumbali ya kumadzulo ya Betelehemu.

⁵² Pamene inu mukukwera, kuchokera kumusi mukulowa mu Yudeya, inu mumakwera pamwamba pa phiri, ndi chipululu cha miyala, dziko labwinja. Ndipo kumalunjika kuchokera ku imodzi ya misewu yayikulu ya Betelehemu, pali kanjira kakang'ono kamene kamakwera pamwamba pa phiri, kamene kamatchedwa msewu, ndipo si koposa kanjira kakang'ono chabe monga momwe ife tingapezere apa, kamene nyama zinali zitapondamo. Chifukwa, kanali kanjira ka abulu, kumene abulu ndi ngamila zimadutsako, zikamapita ku Yudeya, kuchokera ku Betelehemu.

⁵³ Ndipo pamene inu muli pamwamba, mukuchokera ku Yudea, mpaka mu Betelehemu, ndi kutulukira pamwamba pa phiri, pali thanthwe lalikulu liri pamenepo, penapake gawo limodzi mwa magawo atatu a kukula kwa nyumba iyi. Ndipo izo ziyenera kuti zinali cha pamenepo, kumene iwo anaima, atatha kukwera phiri, kuti amupatse mphongolo wamng'onoyo mpumulo. Ndipo Yosefe anali atatopa kwambiri chifukwa iye anali atakankhidwa mwamphamvu tsiku limenelo, kuti akafike ku Betelehemu.

⁵⁴ Chifukwa, panali kulamula kumene kunatuluka kuchokera kwa Herode ndi Kaisara Augustus, kuti munthu aliyense ayenera abwerere kumene anabadwirako, kuti akapereke msonkho. Ndipo misonkho nthawizonse yakhala ili kugwa kwa mafuko onse. Fuko lirilonse limene linayamba lagwapo,

linagwa chifukwa cha misonkho yake. Ndipo iwo anali atalipira msonkho.

⁵⁵ Ndipo, oh, izo zingatengere munthu wa mtima wachitsulo, kuti amupangitse mkazi, mu chikhalidwe chake, kumuchotsa mnyumba ndi kupita kutali ndi kwawo, mmene iye analiri, chifukwa inu mukuona kuti iye anali woti akhala mayi pa nthawi iliyonse. Ndipo iye anali mtsikana chabe, pafupifupi... ndikukhulupirira kuti iye anali mma eyitini, usinkhu wa zaka naintini. Ndipo iye anali atakhala pa bulu wamng'onoyo, ndipo pamene bulu wamng'onoyo ankasimidwa pamene iwo anaima kwa mphindi yokha kuti apumule.

⁵⁶ Ndipo Yosefe akuyenda mpaka pa nsonga, kuchokera kumene iwo anali atayimapo, ndipo nkudzayang'ana pansi mu Betelehemu. Dziko linkadziwa pang'ono kuti usiku umenewo ikanadzaimbidwa pa milomo ya anthu kudutsa mmibadwo imene inali nkudza! Ndipo Yosefe, pamene iye ankayang'ana ndi kuwuwona mzindawo, ndi kukangana kwa anthu, ena otsutsa kuti azipereka misonkho, ndipo ine ndikukhoza kumumva iye akunena chinachake chonga ichi, "Wokonedwa, iwe ukudziwa, ine ndikukaika ngati ife titi tipeze malo pa hotelo, usikuuno, a iweyo. Ine ndikukhoza kuwawona anthu akugona mmisewu ndi kulikonse kumene iwo angakhoze kupeza, kuti akagoneko. Mzinda wadzadza. Ndipo madera onse ozungulira kuno, abwera chifukwa cha msonkho uwu."

⁵⁷ Koma, zachirendo, pamene iye akutembenuka modabwitsidwa, kuti ayang'ane, mkazi wake wamng'ono amawoneka kuti sakanakwanitsa kuti ayankhe. Ndipo pamene iye akutembenuza mutu wake, kuti awone chimene chinali chitachitika kwa iye, iye anazindikira kuti panali kuwala pa nkhope yake, kong'a kumene iye anali asanakuwonapo. Ndipo pansi pa nkhope yake yokonedwa, maso ake anawoneka ngati amakhazikika chamwamba, akuyang'ana mu mlengalenga, ngati kuti panali kuwala kwakumwamba pankhope pake. Ndipo iye akutembenuka ndi kudzamugwira iye pa dzanja.

⁵⁸ Ndipo potsiriza iye akuyang'ana pa iye, ndipo akuti, "Yosefe, kodi waiwona Nyenyezi ija yapachikika kutaliko? Iyo ikuwoneka kuti ndi nyenyezi yokongola kwambiri imene ine ndinayamba ndaiwonapo mmoyo wanga wonse. Iyo ikuwoneka kuti ikuwunikira mudzi wonse wa Betelehemu." Ndipo ine ndikukhoza kumumva iye akuti, "Kuyambira pamene dzuwa limalowa, ine ndayiwona Nyenyezi imeneyo, ndipo Iyo ikuwoneka kuti ikutitsatira ife."

⁵⁹ Yosefe, ine ndikukhoza kumumva iye akunena chinachake chonga ichi: "Inde, wokonedwa, ine—ine ndikuwona chinachake chachirendo, pakuti Iyo ikuwoneka kuti ndi nyenyezi yowala kwambiri mmiyamba monse." Ndipo moonadi uko nkulondola.

Iye ndi Kakombo wa Mchigwa, Nyenyezi
ya Mmawa, (Monga wandakatulo anayikira
iyo.)

Wopambana mwa teni sauzande kwa moyo
wanga.

⁶⁰ Ndipo pamene iye akutenga manja ake, mwachikondi, kudzagwira miyendo ndi mchiuno mwa wokondedwa wake wamng'ono, ndi mkazake, iye anamunyamula iye kuchokera pa buluyo, kudzamunyamula iye, ndi kudzamukhazika iye pansi pa thanthwe, kuti chamoyo chaching'ono cholemedwacho chikhoze kupumula.

⁶¹ Ndipo pamene iye anaika mikono yake mofewa mozungulira mapewa ake, ine ndikukhoza kumumva iye akunena chinachake monga chonchi, "Yosefe, ife tonse tikudziwa kuti zonse izi ndi zachinsinsi. Ife sitingakhoze basi kuzimvetsa izo. Koma, tonse ife pokhala okhulupirira, ife tikudziwa kuti Yehova watisungira chinachake. Ndipo kuti Iye watisankha ife; ndipo wandisankha ine, pamwamba pa akazi a mdziko lero, kuti uthenga uwu ubisidwe mu mtima mwanga." Inu mukuona, dziko linkaganiza kuti ameneyo anali mwana wapathengo woti abadwe, koma Maria ankadziwa chimene chinali choona.

⁶² Ndipo, lero, anthu ambiri amaganiza chinthu chomwecho, kuti, "Anthu amene amulandira Khristu uyu," iwo amaganiza kuti, "iwo ndi mtundu wina wa amisala, kapena munthu wa mbiri yoipa." Koma iwo amene asunga Mzimu umenewo ndi Chikhulupiro chimenecho mu mtima mwawo, iwo amadziwa kumene iwo ali. Palibe chimene chimasokoneza Izo.

⁶³ Mzanga wabwino wa ine anandiimbira ine masiku angapo apitawo, ndipo amayankhula ndi munthu yemwe amaphunzira za kuwerenga maganizo ndi—ndi—malingaliro. Ndipo munthu uyu anali atawerenga bukhu langa, ndipo iwo anati, "Ngati iye ali munthu wauzimu, kodi inu mukudziwa kuti pali ulusi umodzi wokha wawung'ono pakati pa anthu akuya auzimu ndi misala?" Ndipo munthuyo anakhala ngati wadzidzimutsidwa.

⁶⁴ Ine ndinati, "Musaganize kuti izo nzachirendo. Ambuye wathu ankatchedwa wopenga. Ophunzira Ake onse ankatchedwa openga. Ndipo onse amene ankamupembedza Iye ankatchedwa openga. 'Mu njira yomwe zimatchedwa mpatuko,' anatero Paulo wamkulu, 'ndi momwe ndimampembedzera ine, Mulungu wa makolo anga.'" Iwo si amisala. Koma, dziko, kulalikira kwa Uthenga ndi zopusa kwa iwo akuwonongeka. Koma chinamukomera Mulungu, kupyolera mu kupusa uku, kuti awapulumutse iwo amene akanati adzakhulupirire.

⁶⁵ Ndipo pamene iwo, banja laling'ono ili, linakhala pamenepo ndi kumayang'ana kunja kudutsa chigwa chimenecho, ndipo anaiwona Nyenyezi yaikulu iyi ikuwala Kummawa; patali, mazana a mailosi kudutsa zimenezo, mmbuyo uko

kudutsa mapiri, ndi nyanja, uko mu India, uko kunali Amagi akuyang'ana nawonso.

⁶⁶ Tsopano, amuna anzeru awa amene ife tikuwakamba, ankatchedwa... Iwo kwenikweni ndi Amagi, amene ali akasidi amene amayang'ana nyenyezi. Iwo ankatchedwa, pamenepo, "amuna anzeru." Ndipo iwo akadali pobe lero. Ine ndayankhulapo nawo iwo, nthawi zambiri. Ndipo iwo nthawizonse amayenda atatu, chifukwa atatu ayenera kugwirizana. Ndipo atatu ndi kutsimikizira. Ndipo mu India, posachedwapa, ine ndimakhoza kuwawona iwo atakhala mmisewu, ataweramira pansi limodzi, atavala ndendende basi monga Amagi oyamba awa. Iwo samasintha.

⁶⁷ Ndipo iwo ndi opembedza Mulungu mmodzi woona. Iwo ndi ana a Abrahamu, kudzera mwa mkazi wina. Ndipo iwo amakhulupirira kuti kuli Mulungu mmodzi woona. Ndi kangati komwe ine ndawonapo ansembe Achimuhamedi akugunda belu lalikulu monga *chomwecho*, ndi kukuwa, "Alipo Mulungu mmodzi woona ndi wamoyo, ndipo Muhammadi ndiye mneneri Wake."

⁶⁸ Ife timati, "Alipo Mulungu mmodzi woona ndi wamoyo, ndipo Yesu ndi Mwana Wake."

Ndipo iwo amati, "Zikhale kutali kuti Mulungu angakhale ndi Mwana!"

⁶⁹ Ine ndinali nawo mwayi kuwona pafupifupi handiredi sauzande atabwera kwa Khristu, pa nthawi imodzi, chifukwa cha Kukhalapo Kwake ndi chimene Iye anachita mu India.

⁷⁰ Tsopano, Amwenye, amene ife timawatcha amuna anzeru, anali poyamba, mu Baibulo, ankaimiridwa ngati Amedi-o-Persia. Inu mudzazipeza izo mu mutu wachiwiri wa Daniele. Kuti, ndicho chifukwa chake mmishonare amanena kuti, "Ndikovuta kwambiri kumutembenuza wachi Muhammadi kuchoka ku chikhulupiriro chake, kupita ku Chikhristu chifukwa iwo ndi ochokera ku Amedi-o-Persia amene malamulo awo samasintha nkomwe kapena kuswedwa. Ambiri a inu owerenga Baibulo mukudziwa zimenezo, Amedi-o-Persia, kuti iwo sanasinthe malamulo awo. Pamene chinachake, kulengeza kupangidwa, izo zimakhala zamuyaya. Chotero pamene wachi Muhammadi apita ku Chikhristu, chirichonse chimakhala chakufa kwa iye, chifukwa iye waphwanya malamulo awo.

⁷¹ Ndipo amuna awa, iwo ankayembekezera pa Mulungu mmodzi woona, ndipo iwo ankamupembedza Iye mu kuwala kwa moto wopatulika. Ndipo iwo amakhoza kuzungulira moto uwu ndi kuyembekezera pa Ambuye. Ndipo ambiri a iwo anali nazo zoyang'anira, chinachake monga ife tiri nacho lero, ndipo iwo amakhoza kupita ku malo awa kutali mmwamba mmapiri, ndipo iwo amakhoza kuyang'ana kusuntha kulikonse kwa nyenyezi. Iwo amadzinenera, kuti, "Mulungu asanachite chirichonse pa

dziko lapansi, Iye nthawizonse amawonetsera izo kumwamba poyamba.” Ndipo iwo amalondola.

⁷² Nthawizonse, Mulungu amasonyeza izo mwa zizindikiro zakumwamba, poyamba. Pakuti ndi liti limene Iye anachita chirichonse chimene Iye sanachisonyezere chizindikiro chakumwamba, poyamba? Taganizani za zimenezo, mu m’badwo uliwonse umene inu mukufuna kutero, ndipo Mulungu nthawizonse amasonyeza zizindikiro kumwamba, choyamba, Iye asanachite chirichonse pa dziko lapansi. Zimachokera ku chauzimu, kudzagwera mu chachirengedwe, ndipo chimawonetseredwa; m’badwo uliwonse, nthawi iliyonse.

⁷³ Ndipo chotero nthawi iyi siinali yosiyana. Ndipo Amagi anali kuwawona matupi akumwamba amenewo amene anali owoneka, nyenyezi, mwezi, ndi chirichonse chimene iwo ankakhoza kuwona ndi maso awo. Ndipo iwo ankadziwa malo aliwonse, basi pamene nyenyezi iliyonse imakhala. Iwo ankaidziwa kalendala ya mkasidi imeneyo chimodzimodzi basi monga momwe ife timawadziwira Malemba. Ndipo ngati kanthu kamodzi kakang’ono kachoka mmalo, iwo amadziwa izo, pakuti ndi chizindikiro. Ndipo iwo anali akuyang’ana zizindikiro zimenezo, mwatcheru, ora lirilonse la usiku. Iwo ankayang’ana izo. Nzosadabwitsa kuti Mlendo akawonekera mumlengalenga zingawatangwanitse iwo onse! Nzosadabwitsa kuti Mlendoyo anawagwedeza iwo, pang’ono pokha! Chifukwa, iwo ankadziwa iliyonse ya nyenyezi zimenezo, ndipo iwo anaphunzira zimenezo, mwasayansi, ndi kusuntha kulikonse.

⁷⁴ Ndipo iwo ankakhoza kusunkhana pozungulira moto uwu. Ndipo iwo ankawuyatsa iwo ndi mafuta opatulika, ndipo iwo unkayaka, ndipo iwo amakhoza kuyang’ana mmenemo, chifukwa iwo ankakhulupirira, kuti, “Mulungu anali Moto wonyeketsa.” Ndipo Iye ali.

⁷⁵ Inu mukuona, mu Machitidwe, mutu wa 10 ndi ndime ya 35, Lemba limanena kuti, “Mulungu samalemekeza munthu, koma Iye amamulandira munthu aliyense amene angamuwope Iye ndi kumulemekeza Iye, ziribe kanthu chomwe iwo ali.” Ndi inuyo a Methodist, ndi Abaptisti, ndi Apresbateria, Achilutera, kapena—kapena Akatolika, kapena chirichonse chimene inu mungakhale muli. Ngati inu muli woonamtima mu mtima mwanu, Mulungu adzakupatsani inu mwayi, kuti akubweretseni inu mu Kuwala Kwauzimu kwa chifundo Chake. Iye ndi Mulungu, ndipo Iye ndi wokakamizika kudzera mu lonjezo Lake. Ndiye izo zimakhala kwa inu, chimene inu mudzachite mutalandira Iwo; ndiye inu mukhoza kuyima pa chiweruzo. Koma kufikira nthawi imeneyo, inu mulibe choyankhira, inu mukuyenda mu zonse zomwe inu mukuzidziwa.

⁷⁶ Chotero Amagi awa, ndipo iwo amakhoza kukwera, atatha kupembedza pozungulira malo opatulika a motowo, pamene

iwo unkayaka, ndipo amayang'ana mu zowala zake zopatulika, ndi kumadabwa ngati kudzoza kwa Mulungu ameneyo Amene anali Moto wonyeketsa... "Kukhalapo Kwake, dziko lapansi lidzawonongeka." Pamene iye anayang'ana mmenemo, ndiye iye amakhoza kupeza kudzoza kwake. Ndiye iye amakhoza kuyenda kupita mu nsanja, ndipo iye amakhoza kuyang'ana pozungulira, kuti awone ngati chirichonse chinali chitasuntha. Ndipo iwo ankachita izi, chaka ndi chaka, tsiku ndi tsiku, ora ndi ora, zakachikwi pambuyo pa zakachikwi. Iwo ankayang'ana nyenyezi, matupiwo. Ndipo iwo ankatulutsa mipukutu ndipo iwo ankawerenga izo.

⁷⁷ Ndipo izo ziyenera kuti zinali pa usiku winawake uwu, kuti iwo anali kukambirana za—kugwa kwa ufumu ndi kugwa kwa maufumu, ndi momwe kuti dziko linakwera mmwamba kufika mmalo ndi kudzagwanso kachiwiri, ndi zina zotero, kuti panali mpukutu umene unabweretsedwa. Ndipo ilo liyenera kuti linali Bukhu la Daniele. Ndipo iwo anali akukambirana chinachake pamenepo, chimene Daniele ananena, "Padzakhala Mwala wodulidwa kuchokera m'phiri, popanda manja."

⁷⁸ Ndipo izo ziyenera kuti zinali pamene iwo anali kuganizira pa izi, ndipo moto wopatulika ukuyaka, kuti iwo anapezeka akuzindikira kuti panali Mlendo pakati pawo, chinachake chimene iwo sanakhoze kuchiwerengera. Palibe uliwonse wa mipukutu yawo unanena za Iye. Palibe za zolemba zawo zinanena chirichonse chokhudza Iye, koma Iye anali pamenepo! Iwo sakanakhoza kumukana Iye. Iwo ankayang'ana matupi akumwamba, ndipo iwo anadziwa kuti chinachake chauzimu chinali chitachitika.

⁷⁹ Oh, Iye ndi wabwino kwambiri! Iye adzagwira tcheru cha munthu aliyense yemwe Iye anadzozedweratu ku Moyo, mwinamwake mu njira zawo zomwe za kupembedza. Koma Iye ndi Mulungu, ndipo Iye amadziwa mitima ya anthu, ndipo Iye amawayang'anira iwo, ndipo Iye amawatetezera iwo, ndipo Iye amawabweretsa iwo ku malo! "Pamene chakuya chiyitanira ku Chakuya," payenera kukhala Chakuya kuti chiyankhire ku kuitana kumeneko. Ngati munthu akamachitira ludzu chinachake, izo zimasonyeza kuti pali Chinachake kunja uko choti chiyankhire, kuti chithetse ludzu limenelo.

⁸⁰ Monga ine ndakhala ndikunenera kawirikawiri: pasanakhale chipsyepsye pansana wa nsomba, panali madzi choyamba kuti iyo iyambe kusambiramo, kapena iyo siyikanakhala nacho chipsyepsye chosambira nacho. Pasanakhale mtengo woti umere pa nthaka, panayenera kukhala nthaka, choyamba, kapena sipakanakhala mtengo.

⁸¹ Zaka zina zapitazo, ndikuwerenga izo, ine ndinazindikira nkhanu mu nyuzipepala, kumene mnyamata wamng'ono amadya zofufutira za mapensulo ku sukulu. Ndipo tsiku lina amayi

ake anamupeza iye pa khonde lakumbuyo, akudya phedulo la njinga yake. Ndipo iye ankadabwa lomwe linali vuto ndi mwana wamng'onoyo. Iye anamutengera iye ku chipatala, kuti akamupime. Pamene amafufuza thupi lake laling'ono, madokotala anapeza kuti iye ankasowejera salfa. Ndipo salfa amakhala mu rabara. Chotero, pasanakhale chilakolako mu thupi lake, lofuna salfa, panayenera kukhala salfa kuti ayankhire ku chilakolako chimenecho, kapena iye sakanakhala nacho chilakolakocho.

⁸² Ndipo pasanakhale chirengedwe, payenera kukhala Mlengi kuti apange chirengedwe chimenecho.

⁸³ Ndi mwamuna uti kapena mkazi muno lero, mnyamata kapena mtsikana, amene samafuna kukhala ndi moyo? Ndiuzeni ine wachivundi, lero, yemwe safuna moyo, kukhala moyo wosatha, ndipo ine ndikusonyezani inu munthu wamisala yemwe samadziwa, pakuti palibe kanthu kopambana kuposa moyo.

⁸⁴ Kodi inu mungapereke chiyani lero, ngati dziko likanakhala lanu ndi katundu wake yense? Inu mukanalipereka ilo monyadira, kuti mukhale moyo wosatha, ndi kukhala wosauka. Moyo! Ndi angati a inu achikulire omwe mungapereke chirichonse chomwe muli nacho, kuti mubwererenso kukakhala mnyamata kapena mtsikana? Munthu aliyense amawufunafuna iwo. Chifukwa chiyani? Ulipo kwinakwake, kapena inu sibwenzi mukulakalaka nkomwe kuti mukhale nawo iwo.

Nchifukwa chiyani anthu odwala muli muno, lero, ngati inu mulipo? Kodi inu mukufunafuna chiyani? Nchiyani chikukupangitsani inu kubwera ku pemphero? Chifukwa muli chinachake mwa inu! Ziribe kanthu kuti ndinu a mpingo wanji, mtundu wanji wa dzina limene inu muli nalo, izo ziribe kanthu kochita ndi zimenezo. Ndinu munthu. Ndinu cholengedwa cha Mulungu. Ndipo muli Chinachake mwa inu, chimene chimakukokerani inu kwinakwake. Ndipo motsimikiza basi pamene pali chikoka mu mtima mwanu, adotolo mwinamwake atakulepherani inu, kuti ziyembekezo zikadalipobe. Payenera kukhala kuti alipo kasupe wa chuma cha Mulungu, wa Mphamvu Yake yochiritisa, yotseguka kwinakwake, kapena inu sibwenzi muli ndi chilakolako cha Iyo. Iyenera kukhalapo kwinakwake!

⁸⁵ Ngati inu mukhumba kuti mudzamuwone Yesu ameneyo, ngati chinachake chimakupangitsani inu kukhumba kuti mumuwone Yehova, Iye ali kwinakwake kapena inu sibwenzi muli nacho chikhumbo chimenecho. Mulungu ndi wabwino basi kwa inu monga Iye aliri kwa amuna anzeru kapena kwa aliyense. Ngati inu mukumufuna Iye, "Odala ali iwo amene amva njala ndi ludzu la chirungamo, pakuti iwo adzabweretsedwa ku Kasupe ameneyo kumene iwo angakhoze kumwa gawo lokhutitsa."

⁸⁶ Pakhoza kukhala anthu akufa pano. Inu simukufuna kuti mufe, inu mukumverera kuti pali chinachake chimene chatsalira kwa inu. Ndi chifukwa chake inu muli pano. Pakhoza kukhala amisala, pomwe iwe sungathe ngakhale kugwirizanitsa malingaliro ako pamodzi; koma chinachake pansi mwa iwe chikukuuza iwe, “Pali Chinachake chimene chingakhoze kundibwezeretsa ine kachiwiri.” Pakhoza kukhala aziwerewere amene anayendapo mu msewu, mwa manyazi; pakhoza kukhala akazi amene akhala moyo wosalungama kwa amuna awo, ndipo aswa malumbiriro awo a chikwati; pakhoza kukhala amuna amene ali zidakhwa, achita chirichonse chimene chiripo pa kalendala ya tchimo; koma Chinachake chimakuuza iwe kuti Kasupe alipo kwinakwake.

⁸⁷ Inu mukhoza kukhala Mkatolika, inu mukhoza kukhala Myuda, inu mukhoza kukhala chirichonse chimene inu muli, koma ndinu munthu yemwe anapangidwa mu chifanizo cha Mulungu. Ndipo Iye akukokera kwa inu, akukuitanani inu, ndipo inu mukutsogozedwa basi monga amuna anzeru aja ankatsogoleredwa.

⁸⁸ Ndipo pamene iwo anali kuphunzira, ndipo nkumayang’ana kutsidya ndipo anawona Kuwala kuja, iwo samatha kuganizira chimene Iko kunali. Ndipo tiyeni tiganize kuti iwo... Tsiku lotsatira iwo anagona pansi, kuti apite kukagona. Iwo anali akuvutitsidwa, ndipo anakhala akukuwona Iko. Ndipo mmodzi wa iwo ayenera kuti anali ndi loto, Bildadi, ife tinganene kuti iye anali ndi loto. Ndipo analota kuti panali uneneri umene unati, “Padzakhala Nyenyezi ya Yakobo iti idzauke. Ndipo kwinakwake kumeneko, pakati pa Ayuda, kuli mwana Mfumu yemwe ali woti adzabadwe. Ndipo Kuwala uko kumene inu mukukuwona tsopano kudzakubweretsani inu ku Kuwala kwangwiro kumene kudzamuwalitse munthu aliyense wofuna Kuwala, amene adzabwere pa dziko lapansi.”

⁸⁹ Mwaona, ziribe kanthu kuti chinali chipembedzo chiti, ngati iwo amamuwopa Mulungu kwenikweni, Mulungu ali wokakamizika kuti adzawabweretse iwo ku Kuwala uku. Iye amawabweretsa iwo mwanjira yawo yomwe.

⁹⁰ Nthawizina Iye amawabweretsa iwo mwa zosautsa. Nthawizina Iye amawabweretsa iwo... Inu mukudziwa, mmasiku otsiriza ano, Iye ananenera kuti iwo akanadzabwera mwa zosautsa. Iye anapanga mgonero uwu, ndiyeno palibe—palibe wina ati adzabwere, ndiyeno Iye anati, “Mupite mmisewu yaikulu ndi mmisewu, ndipo mukawatenge olumala, osayenda, akhungu, ndi osautsika, pakuti magome Anga adzazadza.”

⁹¹ Iye akuwafunafuna iwo kuchokera ku mayendedwe aliwonse ndi ngodya iliyonse ya moyo, kulikonseko, akuyenda mu Mzimu mmasiku otsiriza ano, kuwabweretsa iwo palimodzi. Zipembedzo zonse, ndi onse amene—amene akufunafuna moyo,

ali nawo ufulu woti awulandire Iwo, kuti ayende mu Kukhalapo Kwake, kwa Umunthu Wake waulemelero, pakuti Iye ndi Mwana wa Mulungu wamoyo, akadali Nyenyezi ya Mmawa ikuwala pakati pathu, monga Iye nthawizonse ankawalira.

⁹² Kuwala komweko kumene kunamukanthira Paulo pansi, pa njira yake waku Damasiko! Wodzipereka mu mtima mwake, kuyesetsa kuti akazunze gulu la anthu amene anali aphokoso kwambiri, akufuula, akupanga kuphokosera kochuluka; iye anapita uko kuti akawakanthe iwo, ndipo iye ankaganiza kuti iye anali kulondola. Ndipo apo panayima Lawi la Moto lija panjira yake, limene linamukanthira iye pansi. Linafuula, “Saulo, chifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?”

Iye anati, “Ndinu Ndani, Ambuye?”

Anati, “Ine ndine Yesu,” Yehova yemwe iye anali naye changu.

⁹³ Iye anali naye changu Yehova. Iye sankadziwa kanthu za Yesu, kokha, “Iye anali a—chigawenga.” Koma Mulungu anamutumiza iye, ndipo iye anadzakhala wamishonare wamkulu kwambiri amene dziko linayamba lamuwonapo. Bwanji? Iye anali wodzipereka; iye ankakhulupirira. Mulungu anamutsogolera iye ndi Kuwala.

⁹⁴ Kodi inu mukuganiza kuti zimenezo zimatipangitsa ife kumverera chiyani lero, monga Akhristu, kuwona ngakhale chithunzi cha Iye? Ndipo ine ndiri naye mmodzi tsopano yemwe amatsutsa zimenezo, mwa mahandiredi a nthawi. Koma Yehova Mulungu yemweyo watumiza Kuwala Kwake, kusanafike Kudza kwa Mwana Wake nthawi yachiwiri, kuti adzatitsogolere ife, kuti adzatitonthoze ife, ndi kuti adzatibweretse ife mu Kasupe ameneyo; kuti ife tikakhoze kusamba ku machimo athu, ndi kukhala oyera mu chirungamo cha Mwana Wake, Ambuye Yesu, ndi kudzakhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, obadwa mwatsopano mwa Mzimu wa Mulungu, umene umasintha.

⁹⁵ Kubadwa kumatanthauza kuti ife tasinthidwa kuchoka ku kuganiza kwathu, tasinthidwa kuchoka ku kachitidwe kathu, tasinthidwa ndi chinachake chimene chinachitika, mkatimu. Palibe chipembedzo mdziko, palibe madzi okwanira, palibepo miyambo yokwanira kapena maulaliki, amene angakhoze kukusinthani inu. Zimatengera Magazi a Mwana wa Mulungu, Yesu Khristu. Inu simungakhozenso kudziyeretsa nokha, pakujowina mpingo, kuposa momwe kambuku angakhoze kunyambita mawanga ake pa iye. Akamanyambita kwambiri, mpamene amawala kwambiri. Iye amangowawonetsera iwo. Pojowina mipingo ndi kuyesetsa kumachita zodziyenereza za inu eni, inu mumangosonyeza chosowa chanu, cha njala mkatimu, chinachake chimene sichinadzazidwe panobe. Siyani kuyesera; ingolandirani. Iye akutsogolerani inu ku Kuwala.

⁹⁶ Ndipo pamene anthu awa anali ndi loto ili, kuti iwo ayenera akamupembedze Mwana uyu, iwo ayenera kupita. Ndipo iwo anali amuna olemera. Ndipo iwo anasonkhanitsa chuma chawo ndi kuchiyika icho mosungira, cha monga lubano, golide, ndi mure. Atatu anapita, ngati mboni. Ndipo iwo anakwera ngamila zawo, ndipo iwo anatulukamo, akuitsatira Nyenyeziyo. Iwo ayenera kuti anapita pamwamba pa phiri, anabwera kumeneko ndipo anadzawoloka Mtsinje wa Tigris pa mphanda, ndi kumatsika mpaka mu chigwa cha Sinara. Ndipo Nyenyezi inali ikuwatsogolera iwo ku Yerusalemu.

⁹⁷ Pakuti, Yerusalemu nthawizonse wakhala ali mpando wachipembedzo wa mdziko, pakuti Mfumu yaikulu inkakhala kumeneko. Munali mu mzinda womwewo, kumene kunali Mfumu Yemwe anakomana ndi Abrahamu akubwera kuchokera kokapha mafumu, ndipo Dzina Lake linali Melkizedeki. “Iye analibe ngakhale abambo kapena amayi; analibe chiyambi cha masiku, kapena mathero a moyo.” Ngakhale mbadwa, Abrahamu, anapereka chakhumi, zachikhumi, kwa Iye. “Wopanda bambo, wopanda amayi; popanda nthawi yomwe Iye anayamba, kapena palibe nthawi yomwe Iye ati adzathe konse.” Ndi Mfumu yayikulu inachokera ku Salemu, kumene kuli ku Yerusalemu.

⁹⁸ Ndipo Nyenyezi inawatsogolera amuna anzeru awa mpaka ku mpando wachipembedzo wa mdziko, koma, chinthu chachisoni chinali, pamene iwo anakafika kumeneko, iwo sanadziwe kanthu za Iyo. Ndipo amuna anzeru awa amapita chokwera-ndi-chotsika mmisewu. Nyenyeziyo, mwamsanga pamene iwo anafika ku Betelehemu... Mwamsanga pamene iwo anafika ku Yerusalemu, Iyo inatulukira, kotero Iyo siyinawatsogolerenso iwo. Kodi Mulungu anali kuchita chiyani? Kungosonyeza... momwe anthu angapezere.

⁹⁹ Komabe, mu zafioloje zathu zonse ndi mipingo yathu yaikulu, ndi—ndi zina zotero, lero, pamene Kuwala kwakukulu kwa Mulungu kwayamba kuwala, mpingo sukudziwa kanthu za Iko. Kodi Vatican ikudziwa chiyani za zinthu izi? Kodi mabungwe a mpingo akudziwa chiyani? Palibe! Ife tiri pa Khristimasi ina.

¹⁰⁰ Amuna awa ankadziwa kuti iwo anali atawona chinachake. Iwo ankadziwa kuti panali chinachake chimene chinali chitachitika. Pakuti, iwo ankafufuza matupi akumwamba, ndipo apa panali Mlendo, ndipo iwo anali atatsogoleredwa mwachirendo. Ndipo tsopano, mu mzinda, iwo akupita chokwera-ndi-chotsika kamsewu kakang’ono kalikonse, akufuula, “Ali kuti Iye amene wabadwa ali Mfumu ya Ayuda? Ife taiwona Nyenyezi Yake Kummawa.”

¹⁰¹ Tsopano, iwo anali Kummawa, iwo anaiwona Nyenyezi Yake Kumadzulo. Koma anati, “Pamene ife tinali Kummawa,”

mahandiredi a mailosi. Mwaona, izo zinawatengera iwo zaka ziwiri kuti apange ulendowo.

¹⁰² Ine ndikudziwa izo zikuthamangitsa zina za zophunzitsa zanu, koma ndi Choonadi. Izo zinawatengera iwo zaka ziwiri kuti apange ulendowo. Iwo sanabwere monga otchedwa Akhristu awa lero, ali ndi mwana wawo wamng'ono mu khola atagona pamenepo, ndipo amuna anzeru akubwera. Izo ndi Chikhristu chamkhutu. Iwo sanabwere kwa khanda lililonse mu khola. Palibe Lemba limene limanena kuti iwo anatero. Iwo anabwera kwa Mwana wamng'ono, usinkhu wa zaka ziwiri. Iye sanali mu khola. Iye anali mnyumba. Werengani Lemba lonse ilo. Koma miyambo ya Chikhristu, oh, iwo alisokoneza dziko lonse ndi zophunzitsa zawo.

¹⁰³ Nchifukwa chiyani Herodi ankawapha ana, usinkhu wa zaka ziwiri, ndiye, ngati Iye anali khanda chabe? Lemba linati iwo anabwera kwa “Mwana wamng'ono,” osati khanda; “Mwana wamng'ono,” usinkhu wa zaka ziwiri. Ndipo Herodi anapita kuti akawaphe ana, kufikira usinkhu wa zaka ziwiri, ndi cholinga chakuti amupeze Iye; akanakhala makanda, iye sibwenzi atatenga usinkhu wa zaka ziwiri, makanda okha.

¹⁰⁴ Sanamupeze konse Iye modyera ng'ombe; iwo anamupeza Iye mnyumba. “Ndipo pamene iwo anafika ku nyumba, iwo anamupeza Mwanayo ndi Maria.” Koma inu mukuona momwe iwo amazipotozera Izo mopotoza.

¹⁰⁵ Nzosadabwitsa! Mausiku angapo apitawo, ine ndinali kulalikira zimene Yesu ananena kwa Afarisi aja, “Inu mwatenga miyambo yanu, ndipo mwapanga malamulo a Mulungu kukhala opanda mphamvu.”

¹⁰⁶ Ndiye iwo akufuula, “Alikuti Mulungu?” Inu mungamukhulupirire bwanji Mulungu pamene inu simukukhulupirira Mawu Ake, ndi kuti, “Alikuti Mulungu wa Baibulo uja?” Bwererani kwa Iye momwe Iye aliri, ndiyo njira yokhayo imene inu muti mudzamudziwire Iye. Njira yake ndi *iyi*.

¹⁰⁷ Iwo anapita chokwera-ndi-chotsika mmisewu, akufuula, “Alikuti Iye? Ali kuti Iye amene wabadwa ali Mfumu ya Ayuda? Pakuti ife tinaiwona Nyenyezi Yake pamene ife tinali Kummawa, ndipo ife tabwera kuti tidzampembedze Iye.”

¹⁰⁸ Oh, ine ndikukhoza kuwawona ena a ansembe akunena kuti, “Akuti, mabwana, inu muyenera kuti munamvetsera kwa gulu la otentheka kwinakwake. Inu muyenera kuti mumamvetsera fioloje ya munthu wina.”

¹⁰⁹ Amuna amenewo akanakhoza kunena kuti, “Ayi, bwana! Ife tinaiwona Iyo ikuyenda. Ife tikudziwa kuti Iyo ndi yeniyeni. Ndipo Iyo yatitsogolera ife mpaka kuno. Koma tikulephera kuti tiyiyeze Iyo panonso, ndipo uno ndi mzinda wa mfumu.”

¹¹⁰ Kodi izo si zachirendo? Mpingo wawukulu kwambiri mdziko, anthu ambiri, komabe iwo samadziwa kanthu za Iyo. Ndipo ngati icho sichiri chikhalidwe chomwecho cha anthu pa dziko lapansi pa Khristimasi iyi, chikhalidwe chomwecho! Palibe amene anali nalo yankho. Iwo samakhoza kupeza yankho.

¹¹¹ Ndipo potsiriza izo zinafika poyipa kwambiri! Awa anali anthu olemera, inu mukanakhoza kudziwa momwe ngamira zawo zinkavalira. Ndipo iwo sanasiye konse msewu umodzi; mngalande iliyonse, iwo ankapita akufuula, “Ali kuti Iye? Ali kuti Iye? Ali kuti Iye?”

¹¹² Ndipo lero ndi mabomba a atomiki akulendewera uko mu zopachikira, lero pamene dziko liri pa mphepete pa kuthetsedwa kwathunthu, ndipo m’badwo uno wa anthu udzawonongedwa mu mphindi; mu kugawanika kwa kukoka kumodzi, pafupifupi fuko laling’ono lililonse likhoza kumiza dziko lapansi.

¹¹³ Mu msonkhano wa asayansi, tsiku lina, iwo anati panali kulunda. Bwanji, bomba la atomiki ndi kamfuti ka chivinikiro, ku chimene iwo ali nacho tsopano. Ndipo mafuko ena ali nazo izo. Ngati Pentagon itangomasula zomwe iwo ali nazo, sipangakhale mzimu wa Khristimasi utatsalira, anthu angakhale akuthamanga m’misewu mwamantha, akukuwa ndi kumalira. Inu simungabisale. Palibe njira yobisalira.

¹¹⁴ Mapeto afika tsopano. Ife tiri pa mapeto, zizindikiro ndi zodabwitsa zikuwonekera, Mesiya akudziwonetsera Yekha mu Mzimu.

¹¹⁵ Mzimu umenewo, ukubwera kumatsika kudutsa m’badwo, kudzipanga Yekha mochuluka ndi mochuluka, mpaka potsiriza anadzabadwa mwa Munthu wangwiro ameneyo.

¹¹⁶ Tsopano kudutsa mu mibadwo ya Methodisti, Baptisti, Presbateria, Pentekoste, ndipo kutsika mpaka kumapeto, ndipo tsopano apa Iwo ukuwonetseredwa basi Iye asanabwerere mu thupi lachithupithupi, Mmodzi wangwiro ameneyo; akuwukokera Mpingo Wake pamodzi, kuwabweretsa iwo kuchokera ku chipembedzo chirichonse, chirichonse, kuwabweretsa iwo kwa Iye, pakuti Iye posachedwapa adzawonekera. Ndipo mipingo ilibe yankho.

¹¹⁷ Chotero Bwalo la Sanhedrin linaitanidwa, ndi Herodi mfumu, ndipo mabwalo amilandu anabwera pamodzi. Ndipo iwo anabweretsa ansembe ndi marabbi. Iwo anati, “Werengani Malemba. Alikuti Mesiya uyu woti abadwe?” inatero mfumuyo.

¹¹⁸ Ndipo chinthu chachirendo, inu mukudziwa kumene iwo anamupeza Iye? Mu uneneri wa Micah. “Iwe, Betelehemu wa Yudeya, kodi sindiwe wochepetsetsa pakati pa akalonga onse a Yuda? Kodi sindiwe woyera wodzigudubuza? Kodi sindiwe—wochepetsetsa wa onse a iwo? Koma kuchokera mwa iwe mudzabwera Kazembe wa anthu Anga.” Ndi kumene iwo anakazipezako izo.

119 Ndipo chotero amuna anzeru, pamene iwo anamva izo, iwo anatuluka pa chipata! Ndipo mwamsanga pamene iwo anachoka pa malo akale, ozizira, obwerera mmbuyo, ofundawo, apo panapachikika Nyenyeziyo kachiwiri. Nyenyezi inali pamenepo. Ndipo Baibulo linati, “Iwo anakondwerera ndi chisangalalo chachikulu zedi.” Oh, ine ndikhoza kunena kuti iwo anafuula pang’ono, pamene iwo anadzapeza, kuti Chauzimu chodala chija chimene iwo anali atachiwona, pamene iwo anatulukamo mu njira zakale, zozizira, zofundazo, Iyo inawonekeranso. Iyo inali ili pamenepo.

120 Ndipo Iyo inawatsogolera iwo ku Betelehemu, kumene iwo anakamupeza Mmodzi ameneyo, kumene Iye, Yemwe anali Emanuele, anali kuleredwa mu shopu ya akalipentala, wosauka. Ndipo iwo anamasula chirichonse chimene iwo anali nacho, ndipo anakachiyika icho pa mapazi Ake. Ndipo iwo anamupembedza Iye chifukwa iwo anadziwa kuti Kuwala kunali kutabwera, ndipo Mpulumutsi wa dziko anali akubadwa. Iwo anapereka, iwo anapereka chirichonse chimene iwo anali nacho, chifukwa Mulungu anali atapereka!

121 “Mulungu analikonda kwambiri dziko lapansi,” mzanga, ameneyo ndi iwe ndi ine, “kuti Iye anampereka Mwana Wake yekhayo wobalidwa, kuti aliyense,” Methodist, Baptist, Presbateria, wachikunja, chirichonse chimene inu muli, “aliyense amene akhulupirira mwa Iye, asawonongeke koma akhale nawo Moyo Wamuyaya,” chimene inu mukuchifunafuna. Khalani nawo Moyo!

122 Ndipo mu maora amene ife tikukhalamo tsopano, ndi kuyandikira kwa kudza kwa Umunthu Wake kachiwiri, ku dziko lapansi, ngati inu mungazindikire Malemba.

123 Taonani yemwe Yosefe anali, tayang’anani pa Mzimu wa Khristu mwa Yosefe. Ankadedwa ndi abale ake chifukwa iye anali wauzimu, iye ankawona masomphenya, koma anakonedwa ndi abambo ake. Kodi ameneyo sanali Yesu? Anagulitsidwa kwa pafupifupi zidutswa sarte za siliva, ndi abale ake, monga Yesu anali. Anaperekedwa, monga Yesu anachitira. Anaponyedwa mu dzenje, kuti wafa, monga Yesu anachitira. Anadzuka ndipo anadzakhala dzanja lamanja la Farao, palibe munthu akanakhoza kubwera kwa Farao kupatula kudzera mwa Yosefe. Ndipo pamene Yosefe akutuluka kuchokera—kuchokera ku dzanja lamanja la Farao, iwo ankakuwa, “Gwadani bondo, pakuti Yosefe akubwera!”

124 Baibulo linanena, kuti, “Pamene Iye adzabwera, monga mphezi imawala kuchokera Kummawa kumapita Kumadzulo, kuti bondo lirilonse lidzagwada, ndipo lirime lirilonse lidzavomereza kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu.” Mafuko onse adzalira ndipo adzanjenjemera pa nthawi imeneyo.

¹²⁵ Chinali chiyani chimenecho? Icho chinawonetseredwa moyandikira, icho chinatulukira mwa Davide, mfumu. Chifukwa, Iye anali zonse Mneneri, Wansembe, ndi Mfumu; ndipo pamene Davide anachotsedwa pa mpandowachifumu ndi kukanidwa, mu Yerusalemu, monga Yesu anachitira, Davide anakhala pa phiri, mfumu yokanidwa, ndi anthu ake omwe, ndipo analira pa Yerusalemu. Ndipo Mwana wa Davide anabwera ndipo anadzakhala pa phiri lomwelo, Mfumu yokanidwa mu mzinda Wake Womwe, ndipo analira pa Yerusalemu, akuti, “Ndi kangati kamene Ine ndikanati ndikufungatire iwe, monga nkhuku imachitira anapiye ake, koma iwe sukufuna ayi.”

¹²⁶ Kodi iwo anamutcha Iye chiyani? “Belezebule, wambwebwe, mzimu woipa.”

¹²⁷ Pamene utumiki Wake unayamba, panali nsodzi wachikulire amene anabweretsedwa kwa Iye, yemwe sankakhoza ngakhale kulemba dzina lake lomwe. Ndipo anayang’ana pa nsodzi wachikulire uja, ndipo Iye anamuza iye chimene dzina lake linali. Ndipo Iye anamuza iye chimene dzina la abambo ake linali. Nsodzi wachikulire uja anamukhulupirira Iye, ndi mtima wake wonse.

¹²⁸ Ndipo wina ataima pamenepo, anatembenuzidwa, dzina lake Filipo. Ndipo iye anapita kuzungulira phiri, mamailosi sarte, ndipo anakampeza mmodzi dzina lake Nataniele, ali pansi pa mtengo, akupemphera. Anati, “Bwerani, mudzawone Yemwe ife tamupeza. Ine ndikudziwa ndinu wokhulupirira wamkulu mwa Yehova. Ine ndikudziwa inu muli. Koma Yehova amalonjeza Mesiya, ndipo ife tamupeza Iye. Iye ndi Munthu wamba chabe, palibe chachikulu chokhudza Iye. Palibe kanthu kofufuma ndi kophunzira za Iye. Iye ndi Kalipentala.” Iye anali—Iye anali Kalipentala, ziwiri zonse zogwirika ndi solo ya munthu.

¹²⁹ Ndipo Nataniele anayang’ana pa iye, anati, “Tsopano dikirani miniti, kodi pangakhale chirichonse chabwino chingachokere ku Nazareti?” Mwaona, iwo anali kuziyembekezera izo kuti zichokera mu Yerusalemu.

¹³⁰ Ndi kumene ambiri a inu mukuyang’anako lero. Musamayang’ane kumeneko. Mdierekezi nthawizonse amagwiritsa ntchito mutu wa munthu ndi maso ake. Mulungu amagwiritsa ntchito mtima wake. Inu muyang’ane ndi kuti, “Oh, izo sizingakhale basi. Ndi zosalingalirika basi. Mwaona, ine ndikhoza kudziwa, ine ndikhoza kuyang’ana pa izo.” Ndi kumene mdierekezi amagona. Mdierekezi amagwiritsa ntchito maso a munthu. Iye anachita zimenezo kwa Eva, pachiyambi, ndipo iye wazichita izo chiyambireni.

¹³¹ Koma, Mulungu amamuza munthu kuti Iye amakhala moyo, mu mtima mwake, ndipo mtima wanu umakupangitsani inu kukhulupirira zinthu zimene inu simungathe kuziwona.

Chifukwa, “Chikhulupiriro ndi thunthu la zinthu zoyembekezedwa, umboni umene inu simukuwuwona.”

¹³² Zedi, mpingo waukulu uwu ndi anthu ake onse aakulu, mamillioni ake onse kuzungulira dziko, akulamulira mphamvu za mdziko, izo ziyenera kukhala zazikulu. Musati muziyang’ana pa izo.

Ndi Mzimu, Mzimu!

Nataniele anati, “Kodi chirichonse chabwino chingabwere?”

Iye anati, “Iwe bwera, udzawone.”

¹³³ Ndipo pamene Iye anamuwona iye akubwera, Yesu anayang’ana pa iye, ndipo Iye anali woti adzachite chizindikiro Chake cha Umesiya pa iye. Iye anati, “Taonani mu Israeli, mwa yemwe mulibemo chinyengo!”

¹³⁴ Iye anati, “Ndi liti pamene Inu munandidziwa ine, Rabbi?” Izo zinamudodometsa iye. “Ndi liti pamene Inu munandidziwa ine?”

¹³⁵ Anati, “Filipo asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansu pa mtengo, Ine ndinakuwona iwe.” Iye akanakhoza bwanji kumuwona iye, mailosi sarte kuseri kwa phiri, dzana lake?

¹³⁶ Pa amene chozizwitsacho chinachitidwa, iye anayang’ana mmwamba ndipo anati, “Rabbi, Ndinu Mwana wa Mulungu. Ndinu Mfumu ya Israeli.”

¹³⁷ Yesu anati, “Chifukwa ine ndachita izi pamaso panu, ndipo inu mukukhulupirira izo, inu mudzawona zazikulu kuposa izi, pakuti idzakhalapo nthawi ikudza pamene inu mudzawona Angelo Akumwamba akutsika.”

¹³⁸ Apo panaima iwo, ngakhale, amene anali anzeru. Iwo anali a mpingo wawukulu, iwo—iwo sakanakhoza kudzivula okha. Iwo anati, “Munthu uyu ndi wambwebwe. Iye ndi Bezezebule. Iye ndi wopenga. Iye ndi Msamariya yemwe ali ndi mzimu woipa pa Iye. Iye wapenga.” Anamulengeza Iye kuti ndi wamisala, poyera.

¹³⁹ Ndipo Yesu anati, “Chifukwa inu mukunena zimenezo kwa Ine, Ine ndikukhululukirani inu chifukwa cha izo. Koma idzafika nthawi pamene Mzimu Woyera uti udzakhale pa dziko lapansi, ndipo udzachita chinthu chomwecho chimene Ine ndikuchita.” “Mawu amodzi motsutsa Iwo sadzakhululukidwa konse mdziko lino kapena mdziko likudzalo.” [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. Taganizani za zimenezo! Mawu amodzi kutsutsa Iwo, ndizo zonse, kukusindikizani inu kwanthawizonse.

¹⁴⁰ Kodi ife tikukhala kuti? Ife tiri pa Khrisimasi kachiwiri. Ndikudabwa ngati chipembedzo chathu chatibweretsa ife pafupi mokwanira kwa Mulungu, kuti ife tikhoza kutsogozedwa mochulukira monga momwe Amagi akanakhoza kutsogoleredwa?

141 Tsopano, kumbukirani, alipo anthu atatu okha pa dziko lapansi, mulimonse: Hamu, Shemu, ndi anthu a Yafeti; ameneyo ndi Myuda, Wamitundu, ndi Msamariya.

142 Tsopano, onse Myuda ndi Msamariya ankamuyembekezera Iye kubwera; osati ife Amitundu. Ife tinali achikunja, otengeka ndi mafano osayankhula, mmasiku amenewo; ndodo pa nsana wathu, chibonga, kupha, kudya zomwe ife tikanakhoza; Amitundu, agalu osayankhula.

143 Koma iwo anali kuyembekezera Mesiya, ndipo analephera kuti awone chifukwa iwo sanazindikire chizindikiro Chake. Ndi chifukwa chake Yerusalemu analibe yankho.

144 Ndi chifukwa chake, lero, iwo alibe yankho. Mulungu ali nalo yankho, yekha.

145 Tayang'anani pa izi mphindi chabe, monga iwo anali. Panali gulu lina la anthu lomwe linkamufunafuna Iye, lomwe liri mu Yohane Woyera 4, ndiro Asamaria. Iwo ankakhulupirira kuti kunali Mesiya wakudza.

146 Chotero kumbukirani, Iye sanachite chizindikiro chimenecho nthawi ina pamaso pa Amitundu, Asamaria okha ndi kwa—ndi kwa Ayuda, kwa amene anali kumuyembekezera Iye kuti abwera. Ndipo iwo sanamukhulupirire Iye, ndi zimenezo; ena a iwo anatero, ena sanatero.

147 Ndipo pamene Iye anabwera ku Samaria, Iye anawatumiza anthu kutali, ophunzira Ake, apite mu mzinda. Iye anayembekezera. Chifukwa, Iye anawauza iwo, “Pitani mukagule chinachake choti tidye.” Zinali pafupifupi nthawi ino ya tsiku, ine ndikuganiza.

148 Pamene iwo anali atapita, a—mkazi wokondeka anatulukira ku chitsime, kuti adzatunge madzi ena. Oh, ife timamutcha iye wachiwerewere. Mwinamwake iye anali. Chabwino, tiyeni tinene kuti iye anali—mkazi wowoneka wokondeka. Iye anabwera ku chitsime ichi, kuti adzatunge madzi ena. Ndipo iye anamva liwu, linati, “Mkazi, ndibweretsere Ine akumwa.”

149 Ndipo iye anayang'ana pozungulira, ndipo apo panakhala Myuda. Tsopano, apo panali tsankho pamenepo, iwo analibe kudyerana kulikonse. Ndipo iye anati kwa Iye, iye anati, “Bwanji, Inu, Myuda, mukundifunsa ine, mkazi wa Chisamariya? Ife tiribe chochita wina ndi mzake. Si zolondola kuti Inu mundifunse ine zimenezo.”

150 Iye anati, “Koma, mkazi, ngati iwe ukanadziwa Yemwe iwe ukuyankhula naye, iwe ukanandipempha Ine Madzi.”

151 Anati, “Chiri kuti... Kodi Inu mukawapeza kuti madzi aliwonse,” anati, “Inu mulibe chinthu choti mutungire, ndi zina zotero.”

152 Ndipo Iye anapitirira ndi zoyankhulanazo, pamene ulendo unali kupitirira. Potsiriza, Iye anati kwa iye, Iye anagwira

pamene vuto lake linali. Iye anati, “Mkazi, pita ukamutenge mwamuna wako ndipo mubwere kuno.”

Iye anati, “Ine ndiribe mwamuna aliyense.”

¹⁵³ Anati, “Uko nkulondola. Iwe wakwatiwa ka faivi, ndipo mmodzi yemwe iwe ukukhala naye tsopano si mwamuna wako.”

¹⁵⁴ Penyani chimene iye ananena. Iwo anali kuyembekezera Mesiya, inu mukudziwa. Iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri.” Ndi inu pamenepo. “Ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri. Ife tikudziwa, pamene Mesiya adzabwera, Iye adzatiuza ife zinthu izi. Chizindikiro cha Mesiya, ife tikudziwa kuti Mesiya adzachita izi pamene Iye adzabwera. Koma Ndiwe basi...muli ndi zikang’a m’manja mwanu. Ndinu Kalipentala, ndi Myuda. Koma Inu mukuyenera kukhala mneneri, kapena Inu sibwenzi mutakwanitsa kuchita izi. Koma pamene Mesiya adzabwera...Ife tikumuyembekezera Iye pano. Pamene Iye adzabwera, Iye adzachita izi.”

Yesu anati, “Ine ndine Iye, amene akuyankhula ndi iwe.” Oh, mai!

¹⁵⁵ Iye anagwetsa mtsuko wa madzi umenewo. Mu mzinda iye anapita, ndipo anati, “Bwerani, mudzamuwone Mwamuna Amene wandiuza ine zinthu zimene ine ndachita. Kodi uyu si Mesiya?” Ndipo mzinda wonsewo unatulukira ndipo unakhulupirira pa Iye, inde, chifukwa chizindikiro chimenecho chinachitidwa. Mipingo inalibe yankho, koma odzichepetsa mu mtima anayang’ana kwa Mulungu.

¹⁵⁶ Lero, ine ndikudabwa ngati chipembedzo chathu chatibweretsa ife ku Luntha limenelo? Kuzindikira kuti siziri mu zafioloje zathu zopangidwa ndi anthu zomwe ife tikuyesera kuphunzitsa, koma izo ziri mu Mphamvu ndi chiwukitsiro cha Yesu Khristu, ndi Mzimu Woyera mdziko lero. M’bale, mlongo, mu ora lotsiriza lino, pamene izo zikubwera ku mapeto a nthawi, mufufuze miyoyo yanu, mufufuze momwe inu mukuimira ndi Mulungu.

¹⁵⁷ Ndi Khristimasi. Zonyezimira zonse ndi kumatsika mu msewu wa Santa Claus, zopeka za Chijeremani, mwambo wa Chikatolika, palibepo kachidutswa kamodzi ka izo kali kowona, ndipo izo zimatengera malo a Yesu Khristu mmitima ya Achimereka ochuluka kwambiri. Khristimasi siimatanthauza Santa Claus, Khristimasi imatanthauza Khristu, osati munthu wina wokhala ndi kaliwo mkamwa mwake ndi kumatsika chotulutsira utsi! Kumaphunzitsa ana anu zonga zimenezo, mumayembekezera kuti iwo akadzakula adzakhala otani? Muziwauza iwo choonadi, osati pa nkhani ina yopeka. Muziwauza iwo kuti kuli Mulungu wa Kumwamba Yemwe anamutumiza Mwana Wake, ndicho chimene Khristimasi imatanthauza, ndipo Iye ali pafupi kubwera kachiwiri.

¹⁵⁸ Ndipo pamene kupsyinjika kukuyamba kubwera pa dziko lapansi, mdierekezi watulutsa zinthu zake, mwa maso, zomwe inu mungakhoze kuziwona, zonyezimira, ndi zina zotero. Mulungu watulutsamo Wake, umene uli Mzimu, umene inu simungathe kuwuwona, koma inu mukukhulupirira.

¹⁵⁹ Yerusalemu analibe yankho. Jeffersonville alibe mayankho; Louisville alibe, Amerika alibe, ngakhale dziko liribe.

¹⁶⁰ Mulungu ali nawo mayankho, ndipo Iye walonjeza kuti Iye akanadzawawonetsera iwo. Ndipo ine ndikulengeza kwa inu kuti Yesu yemweyo, Amene anabadwa zaka naintini handiredi, ali moyo lero, kuchokera ku chiukitsiro, ndipo ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

¹⁶¹ Kodi inu mwaulemu mukukhulupirira izi ndi mtima wanu wonse? Ngati inu mukukhulupirira zimenezo...Ndipo mwinamwake inu simunazilandirepo konse zimenezo, koma, Iye asanachite chinthu chimodzi kuti adziwonetsere Yekha, kodi inu mungakweze manja anu? Pokweza manja anu, pamene aliynse waweramitsa mitu yawo, kodi mungakweze manja anu ndi kuti, “M’bale Branham, mundipempherere ine. Ine ndikukhulupirira kuti icho ndi Choonadi. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti mwanjira ina imzake, mwachinsinsi, ine ndatsogoleredwa ku malo aang’ono akale awa kuno pa ngodya mmawa uno. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Mzimu wa Mulungu wamoyo uli pano tsopano. Ine ndikufuna kuti ndimupembedze Iye. Ine ndikweza dzanja langa.” Mulungu akudalitseni inu. Ndizo zabwino. Oh, mai! Anthu twente kapena sarte, mchipinda chino.

¹⁶² Wokondedwa Mulungu, Inu mukuwaona manja amenewo, ndipo Inu mukumudziwa aliyense wa iwo. Ndipo iwo ali mukusowa. Ndipo sibwenzi atakweza konse dzanja limenelo kupatula Chinachake chitakhala pafupi ndi iwo, Yemwe anali wamkulu kuposa iwo; iwo bwenzi akupitirira mu njira zawo zomwe. Koma iwo akhulupirira, pakumva Mawu. Malemba athu amatiuza ife, Ambuye, Malemba Anu Oyera, kuti, “Chikhulupiro chimadza pakumva, ndipo kumva Mawu a Mulungu.” Ndipo Icho ndi chongungundika, komabe, mwanjira yophweka, a—njira yokhayo imene ife tikuyenera kuwapereka Iwo kwa anthu, iwo awakhulupirira Iwo. Ambiri, manja ambiri anakwera mmwamba. Ine sindikudziwa aliyense wa iwo. Inu mukuwadziwa iwo onse. Koma ine ndikudziwa kuti mkati mwa iwo, iwo akulamuliridwa ndi kulamuliridwa ndi mzimu, ndipo mzimu uwo umenewo umene uli mwa iwo unati, “Inu mukulakwitsa.”

¹⁶³ Ndipo pali Mzimu wina umene waima ndi iwo, ukuti, “Ndilandireni Ine. Ndine Mpulumutsi wanu.” Ndipo iwo anaswa malamulo onse a sayansi, pokweza manja awo. Chifukwa, muli Mulungu mmenemo, Amene anapanga malamulo a sayansi,

ndipo manja awo anakwera mmwamba, kuti iwo amafuna kufikira mmwamba, mwa chikhulupiriro, kuti amugwire Mpulumutsi, ndi kumulandira Iye ngati Mpulumutsi wawo. Iwo achita zimenezo mmawa uno, Ambuye.

¹⁶⁴ Ndipo muwalandire iwo mu Ufumu Wanu, pakali pano. Iwo ndi zikho za Uthenga. Ine ndikupemphera kuti Inu muwalandire iwo mu Kukhalapo Kwanu, mu Ufumu Wanu. Ndipo mulole iwo akakhale miyoyo yosangalala kuno, akuyembekezera Kudza kwa Ambuye Yesu pa nthawi iliyonse, pamene iwo akuwona tsiku likuyandikira, ndi zizindikiro ndi zodabwitsa, chifukwa Iye akuyandikira, pafupi. Iye ali pa njira Yake.

¹⁶⁵ Pamene Rabekah ananyamuka, kukwera pa ngamila, ndipo anapita kukakumana ndi wokondedwa wake, Isaki. Ndipo Isaki anali atachoka kale—msasa, ndipo anali kunja mminda, pa nthawi yakumadzulo, pamene iye anamuwona iye akubwera. Icho chinali chikondi pa kupenya koyamba. Iye analumpha kuchoka pa ngamira, ndipo anathamangira kukakumana naye iye. Iye anatengedwera mu hema wa Abrahamu, ndipo kumeneko anakhala wolowa, ndipo analandira zinthu zonse.

¹⁶⁶ Mulungu, ife tikuzindikira kuti ndi nthawi yamadzulo tsopano. Inu munati kudzakhala Kuwala, kuti Mzimu Woyera udzakhala pano pa dziko lapansi ndipo akanadzakhala akudziwonetsera Yekha mu kagulu kakang’ono kamene Inu munasankha mwa chisomo Chanu. Ine ndikupemphera tsopano kuti Inu—Inu mudziwonetsere Nokha mochuluka kwa aliynse. Ndipo mulole iwo apulumutsidwe ku machimo awo.

¹⁶⁷ Ndipo mulole iwo abwere kwinkwake ku—kasupe, kasupe wa padziko lapansi, iwo atatha kubwera Kumwamba, ndi kubatizidwa mu Dzina la Mwana Wanu wokondedwa, Ambuye Yesu; kuchapa machimo awo, kuitanira pa Dzina la Ambuye. Mulole iwo alandire Mzimu Woyera, ndi kuikidwa pamalo akuti azisewera gawo lawo la sewero lalikulu ili limene likukonzekera kuti lichitike.

¹⁶⁸ Ife tikukhulupirira kusonkhana kwathu mmawa uno, Atate, kunali mu dera Lanu lanzeru. Palibe chirichonse chopusa, kwa Inu. Chirichonse, chirichonse chimene Inu mumapereka, ndi changwirow. Amuna ndi akazi anabwera kuchokera ku madera osiyanasiyana a dzikoli, akhala muno. Inu munawabweretsa iwo mwa Mzimu Wanu, mwanjira yachinsinsi. Iwo akukhulupirirani Inu. Alandireni iwo tsopano. Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikuwapereka iwo kwa Inu.

¹⁶⁹ Tsopano, Ambuye, mulole Mzimu Woyera Wanu ubwere kuti udzachiritse odwala, kuti amene atembenezidwira kwa Inu atsopano awa, akhoze kuzindikira kuti ife sitikungoyankhula chabe za Baibulo lomwe lakhala mbiriyakale. Iyo ndi yamoyo, tensi yatsopano, pakali pano. Iye ndi Ambuye Yesu yemweyo.

¹⁷⁰ Tsopano muloleni Iye abwere, Ambuye, ndipo adzatenge thupi lathu, matupi athu, pamene ife tikutsegula mitima yathu. Chotsani kukaikira konse ndi chidziko chonse. Ndipo mungolola Mzimu Woyera uyenderere kudutsa mwa ife, kuti Inu mukhoze kugwira ntchito chifuniro Chanu pakati pathu, ngati zotengera zoyera. Osati chifukwa chakuti ndife oyera mwa chirungamo chathu chomwe, koma chifukwa ife takhulupirira pa Iye Amene watitsuka ife, Ambuye Yesu; ndipo wachita ndi kuchita—zinthu zimene Inu munachita pamene Inu munali kuno pa dziko lapansi, kuti otembenezidwa atsopano awa akhoze kuwona kuti Inu mukadali Ambuye Yesu. Inu simuli wakufa. Koma Inu munawukanso, zaka naintini handiredi zapitazo, ndipo muli wamoyo lero, kukwaniritsa lonjezo lirilonse limene Inu munapanga. Amen.

¹⁷¹ Ine ndikudziwa kuti si nyimbo ya Khrisimasi, koma iyo ndi nyimbo ya mitima yathu, imene ife timaikonda; tsopano pakuti uthenga watha, wokhala ngati wodula, zina zotero, ndiyo njira yokhayo.

¹⁷² Chimene maguwa athu akusowa lero si chipembedzo chonunkhira ichi kuno. Iwo akusowa Choonadi. Choonadi, kulalikirira Icho kuchokera mu Baibulo! Osapanga kutanthauzira kosiyana kulikonse. Kungonena Iwo, chimene Baibulo limanena. Mulungu ndi wokakamizidwira ku Mawu Ake. Ngati Iye sawaikira kumbuyo Mawu Ake, ndiye Iye si Mulungu, kapena Iwo si Mawu Ake, mmodzi. Koma Iye adzasamalira Mawu Ake.

¹⁷³ Tsopano, basi ife tisanapempherere odwala, tiyeni tiyimbe nyimbo yabwino yakale iyi, anthu nonse inu, limodzi, nonse a inu.

Ine ndidzamyamika Iye, ine ndidzamyamika
Iye,
Kuyamika Mwanawankhosa wophedwera
ochimwa;
Mpatseni Iye ulemelero anthu inu nonse,
Pakuti Magazi Ake atsuka banga lirilonse.

¹⁷⁴ Kodi inu mungatipatse ife poyambira, mlongo? Aliyense, pamodzi tsopano, tonse, aliyense!

Ine ndidzamyamika Iye, ine ndidzamyamika
Iye,
Kuyamika Mwanawankhosa wophedwera
ochimwa,
Mpatseni Iye ulemelero anthu inu nonse,
Pakuti Magazi Ake atsuka banga lirilonse.

¹⁷⁵ Ine ndikudabwa. Izi si zosinjirira, uku ndi kungofotokoza basi. Ana, ndife ana. Pamene inu muyamba kuganiza kuti inu mwakula, mwa Mulungu, zimenezo zisonyeza kuti inu simunafike paliponse. Nthawizonse muzikhala muli mwana, Iye akhoza kukutsogolerani inu. Koma pamene inu mukudziwa

zochuluka kumuposa Iye, inu mukuyesera kumutsogolera Iye. Mukuona? Musiyeni Iye azitsogolera. Tiyeni tingotseka maso athu ndi kukwezera mmwamba manja athu, ndi kuweramitsa mitu yathu, ndi kuyimba iyo kamodzinso.

Ine ndidzamyamika Iye, ine ndidzamyamika
Iye,
Kuyamika Mwanawankhosa wophedwera
ochimwa;
Mpatсени Iye ulemelero anthu inu nonse,
Pakuti Magazi Ake atsuka banga lirilonse.
Kuchokera ku khola la Betelehemu kunabwera
Mlendo,
Pa dziko lapansi ine ndikufuna kukhala monga
Iye;
Monse kudutsa ulendo wa moyo kuchokera
padziko kupita ku Ulemelero
Ine ndikungopempha kukhala monga Iye.
Kungokhala monga Yesu, basi kukhala monga
Yesu,
Pa dziko lapansi ine ndikufuna kukhala monga
Iye;
Monse kudutsa ulendo wa moyo kuchokera
padziko kupita ku Ulemelero
Ine ndikungopempha kuti ndikhale monga Iye.

176 “Zinthu zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita.”

177 Kodi inu simukanakonda mukanakhala mutaima pamenepo pamene Iye ankanena kwa mkazi wa vuto la magazi? Iye anabwera akudzipotokola kudutsa mu unyinjini, iye anakhudza chovala Chake, “Pakuti iye ananena mwa iyeyekha, ‘Uyo ndi Mwana wa Mulungu. Ngati ine nditangokakhudza chovala Chake!’” Tsopano, chovala cha Chipalestina chimalendewera momasuka, ndipo chimakhala ndi chovala chamkati. Iye... Iye sanamverere kukhudza kumeneko, pakuti Iye anatsimikizira izo. Iye anakhudza chovala Chake, ndipo anathamangira mmbuyo mwa omvetsera.

178 Yesu anaima, ndipo anati, “Ndani wandikhudza Ine? Ndani wandikhudza Ine?”

179 Petro anamudzudzula Iye, anati, “Ambuye, aliyense akukukhudzani Inu, akugwedeza manja Anu, akukusisitani Inu, ndi chirichonse. Aliyense wakugwirani Inu, ndipo nchifukwa chiyani Inu mukunena chinthu ngati chimenecho?”

180 Iye anati, “Koma Ine ndafooka. Ukoma wachoka mwa Ine. Winawake wandikhudza Ine.”

181 Ndipo Iye anayang’ana pozungulira, pa omvetsera, ndipo Iye anamupeza iye. Ndipo Iye anamuza iye kuti anali ndi

vuto la magari pamenepo, ndipo chikhulupiriro chake chinali chitamuchiritsa iye.

¹⁸² Kodi inu simukanakonda kukhala monga choncho? Simukanakhoza kuganiza za chirichonse chokulirapo.

¹⁸³ Mwamuna anayenda napita kwa Iye. Iye anati, “Dzina lako ndi Simoni. Dzina la abambo ako ndi a Yonasi.” Oh!

ine ndikungopempha kuti ndikhale monga . . .

¹⁸⁴ Kodi ndi zotheka? Iye anati, “Zinthu izi zimene Ine ndikuzichita! Ndipo komabe kanthawi pang’ono, ndipo dziko . . .” Tsopano, *dziko* kumeneko, mu mawu a Chigriki, ndi *kosmos*, chimene chimatanthauza “dongosolo la mdziko,” osati dziko lapansi, “dongosolo la mdziko.” “Kanthawi pang’ono, ndipo dziko silindiwonanso Ine; komabe inu mudzandiwona Ine,” ameneyo ndi wokhulupirira, “pakuti Ine,” ndipo *Ine* ndi puronauni ya umwini, “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumalekezero a dziko lapansi. Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita. Zochuluka kuposa izi inu mudzazichita, pakuti Ine ndikupita kwa Atate Anga.” Odalitsidwa, Malonjezo opatulika sangakhoze kuswedwa. Yesu anati, “Palibe Lemba lingakhoze kuswedwa.”

Chotero kukhala monga Yesu . . .

Kodi Iye ali pano?

. . . Yesu,

Basi mu chikhalidwe cha kupembedza tsopano.

Padziko ine ndikufuna kukhala monga Iye;
Monse kudutsa ulendo wa moyo kuchokera
padziko kupita ku Ulemelero
Ine ndikungopempha kuti ndikhale monga . . .

¹⁸⁵ Kodi inu mungalingalire Iye akuyenda mu Galileya? Apo pali Afarisi aja, ananena mu mtima mwawo, “Iye ndi Bezezebule.” Iwo sananene konse izo mokweza, koma Iye anazindikira malingaliro awo. Malemba amanena zimenezo? Iye anazindikira malingaliro awo.

¹⁸⁶ Iye anati, “Inu mukayankhula zimenezo motsutsa Ine, Ine ndikukhululukirani inu. Koma idzafika nthawi pamene Mzimu Woyera uti udzachite zinthu zomwezo. Musati mudzayankhule motsutsa Iwo.”

¹⁸⁷ Kungokhala monga Yesu! Ndi angati mwa omvetsera apang’ono awa mmawa uno akukhulupirira kuti Iye wauka kwa akufa, Iye ali moyo lero, ndipo Iye ali yemweyo, kuti asunge lonjezo lililonse? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi]. Zikomo inu. Izo zimabweretsa Kukhalapo Kwake.

¹⁸⁸ Ambiri a inu mukuchidziwa chithunzi cha Mngelo wa Ambuye, uko pamwamba pa pamene ine ndaima. Ife tiri nazo izo kuchokera ku Germany, Switzerland, kulikonse kumene iwo

amajambula izo. Iwo anajambula china tsiku lina. Ndi chinthu chopambana kwambiri chimene ine ndinayamba ndachiwonapo. Ine ndidzachitengera icho ku tchalitchi, nthawi yotsatira ndikadzabweranso. Chiri kwa—akuluakulu amdziko tsopano, kuti afufuze ngati panalibe kulowererana zithunzi, ndi momwe zimayikidwa pansi pa kuwala kwa ultra-ray, ndi zina zotero, kuti awone. Mngelo wa...chithonhozo chachikulu chimene ine ndakhala nacho kuyambira pamene Iye anakomana nane; kudziwa kuti ife tiri pa nthawi yotsiriza.

¹⁸⁹ Ndine munthu, ndipo mulibe chinthu chabwino mwa munthu. Koma ngati munthu angakhoze kutsegula mtima wake ndi kumolola Mulungu kuti amuyeretse iye, ndiye si... Mulungu ali ndi manja okha, iwo ndi manja anu ndi manja anga; maso Ake ndi maso anga ndi maso anu, chifukwa Iye ndi Mzimu. Koma Iye akhoza kugwira ntchito kudzera mwa ife, kuti akawonetsera ndi kuchita chifuniro Chake.

¹⁹⁰ Ine ndimati ndikuitanireni inu kuno mu mzere wa pemphero. Ine ndasintha malingaliro anga. Ine ndikukhulupirira kuti Kukhalapo kwa Ambuye Mulungu kuli pano. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Iye akhoza kuchita chimodzimodzi basi momwe Iye ankachitira pamene Iye anali kuno kalelo, kapena Iye si Mulungu. Ndi anthu angati...

¹⁹¹ Pali nkhope zambiri pano zimene ine sindikuzidziwa. Ine sindimakhala kuno; ngakhale ambiri a inu mukhoza kumabwera ku tchalitchi kuno, ine sindikukudziwani inu. Koma ndi angati muno, amene ali osowa, ndipo inu mukudziwa kuti ine sindikukudziwani inu, kwezani mmwamba manja anu; nonse muli mchipinda chino, mukudziwa. Makamaka ndi kutsogolo kuno, pafupifupi aliyense amene ali kutsogolo, alendo kotheratu.

¹⁹² Ndiye ngati Yesu alimoyo, ndipo Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ndipo ngati inu muli ndi—chosowa cha chinthu chirichonse, Lemba limati...Tsopano, osati Chipangano Chakale; Chipangano Chatsopano! Chipangano Chatsopano, Bukhu la Ahebri, linati, “Yesu Khristu ndi Wansembe Wamkulu pakali pano.” Aliyense amadziwa chimene wansembe wamkulu ali? “Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu.” Wansembe wamkulu ndi woti azipanga chitetezero mu Kukhalapo kwa Mulungu. Yesu akuyima ngati Wansembe Wamkulu, kuti azipanga chitetezero, ndipo Iye akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu. Tsopano, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; ndipo ngati mkazi anamukhudza Iye kumbuyo uko, ndipo Iye anapotoloka ndipo anamuuza iye; ndipo Bartumeyo wakhungu atayima pa chipata, mayadi firii handiredi kuchokera kumene Iye anali, akufuula, “Ndichitireni ine chifundo!”

¹⁹³ Ndipo anthu akumuseka Iye pamene Iye ankadutsa, Iye

ndi mutu Wake cha ku Kalvare, akupita ku Yerusalemu, kuti akaperekedwe. Ndipo ansembe amenewo akuti, “Ukuti, Iwe amene unawukitsa wakufa! Ife tiri ndi manda odzadza ndi iwo kuno, tiyeko ndipo ukawadzutse iwo. Ife tikukhulupirira Iwe.” Gulu lomwelo limene linati, “Tsika pa mtandapo, (Ndiwe ‘Mwana wa Mulungu’), ndipo ife tikukhulupirira Iwe.”

¹⁹⁴ Mukuwawona otsutsa amenewo? Iwo nthawizonse akhalapo nawo iwo. Osadziwerengera, kuchita maere anu ndi mtundu umenewo. Mulungu asalole! Mtengereni Mulungu mu mtima mwanu kuti muzikhoza kumuwona Iye ndi kumudziwa Iye.

¹⁹⁵ Koma wopemphetsa wosauka uyu, wakhungu wachikulire atayima pamenepo, anati, “Inu Mwana wa Davide, ndichitireni ine chifundo.” Ndipo chikhulupiriro chake chinamuimitsa Yesu. Yesu anatembenuka ndipo anayang’ana mpaka Iye anamupeza iye, anamuza iye kuti alandire kupenya kwake.

¹⁹⁶ Yesu yemweyo ali moyo! Ngati...Ndi chaubwino wanji Mulungu mbiriyakale, Iye siali...ngati Iye siali Mulungu yemweyo lero?

¹⁹⁷ Zimachita ubwino wanji izo, kuyesa kuti munthu atenthedwe pomulozera iye ku moto wopentedwa? Moto wopentedwa sungathe...Umenewo ndi moto wa mbiriyakale. Inu mukuti, “Si moto wopentedwa, M’bale Branham, ndi chithunzi cha moto umene unachitikadi.” Inu simungakhoze kutenthedwa ndi chithunzicho. Icho ndi chinachake chimene chinakhalapo. Nanga bwanji tsopano?

¹⁹⁸ Iye ali yemweyo dzulo, kapena Iye...ndi lero, kapena Iye si Mulungu yemweyo. Kodi inu simukukhulupirira zimenezo?

¹⁹⁹ Tsopano mmodzi aliyense wa inu mungokhala molemekeza kwenikweni. Ngati izo ziyenera kukhala kuti ine ndikanati ndiyankhule, ine ndiribe njira yokudziwirani inu. Mulungu akudziwa mtima wanga. Koma ngati Yesu angabwere ndi kudzatenga thupi langa, ndi kudzatenga...Ziribe kanthu kuchuluka kwa momwe Iye angatengere wanga, ngati Iye satenga inu, inunso. Inu muyenera kukhulupirira zimenezo. Pakuti, kumbukirani, izo zimangochitika pamene inu mukukhulupirira. Ngati Ambuye Yesu angabwere ndi kudzachita zimenezo, ndipo inu nkudzakhudza chovala Chake, mukuti, “Ambuye, ine ndikusowa. Ndiroleni ine ndikukhudzeni Inu, Ambuye.”

²⁰⁰ Ndiye ngati inu mumukhudza Iye, ngati Iye ali Wansembe Wamkulu yemweyo, Iye adzachita mwanjira yomweyo imene Iye anachitira pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi. Nkulondola uko? Ngati izo zitachitika mwanjira ina iliyonse, ndiye ndi chinthu cholakwika, inu munakhudza chinthu cholakwika. Izo ziyenera kukhala zofanana, ziyenera kumachita mwanjira yomweyo. Ndiye ngati inu mungakhoze kukhudza chovala

Chake, monga mkazi anachitira yemwe anakhudza chovala Chake, kodi Iye sangachite chinthu chomwecho?

²⁰¹ Ngati izo zitachitika kuti ine... Ngati ena a anthu inu amene mumabwera ku tchalitchi kuno, kotero kuti inu mudziwe, ine—ine sindinena kanthu kwa inu. Icho chiyenera kukhala chikhulupiriro chanu, chifukwa ichi ndi—ichi ndi... Ndine... Ine ndikufuna alendo. Ine ndikutangani inu pakapita kanthawi, ngati Ambuye alola. Ine ndikufuna... Ine ndikubweretsani inu kuno pa nsanja, ndikupempherani inu.

²⁰² Ine ndikufuna alendo amene abwera kuchokera kunja kwa mzinda. Ngati inu anthu a kunja-kwa mzinda, inu muli kuno mmahotelo ndi mmamotelo, ndi zinthu, mukuyembekezera. Zedi, mwabwera kuchokera ku dziko lonse, mwanjira imeneyo. Iwo amawakonda Ambuye. Iwo amamukhulupirira Iye. Ndipo iwo—iwo amawerenga mu Baibulo kuti Iye akuyenera kuchita izi mmasiku otsiriza.

²⁰³ “Ndipo palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye,” anatero Yesu. Inu simungakhoze kubwera, palibe chifukwa choyesera kuti muchite chirichonse kupatula Mulungu atakukokerani inu. Pamene Mulungu akukokani inu, ndiye inu mudzabwera. “Ndipo iye amene abwera kwa Ine, Ine sindidzamtayira konse iye kunja.”

²⁰⁴ Tsopano inu mungokhala ndi chikhulupiriro ndipo mukhulupirire tsopano. Ndipo mukhale molemekeza kwenikweni, ndipo mukhale chete mphindi yokha. Mpatсени Mulungu tcheru chanu. Pempheerani, mukuti, “Ambuye Mulungu, mundilole ine ndikhudze chovala Chanu. Ndine wodwala. Ndine wosowa. Ine ndiri ndi chosowa. M'bale Branham sakundidziwa ine, iyi ndi nthawi yoyamba yomwe ine ndayamba kumuwona bamboyo. Koma ine ndikufuna kuti nditsimikizire kwa inemwini kuti Inu mukadali Yehova, kuti Inu mukadali Yesu yemwe iye akumukamba. Ndipo ine ndikukhulupirira Kuwala kwachinsinsi uku kumene dziko likukukamba lero, ine ndikukhulupirira Iko ndi Inuyo. Ndipo Ndinu Mmodzi yemweyo amene wanditsogolera ine kuno. Tsopano kodi ine ndipeza chiyani? Mundirole ine ndimupeze Iye, Ambuye, Yesu yemweyo amene iwo amupeza. Ndiroleni ine ndimupeze Iye.” Tsopano mungopenya ndi kuyang'ana.

²⁰⁵ Ine ndiribe njira nkomwe yodziwira mpaka Mulungu ataululira izo. Ndipo pamene Mulungu awulula izo, ndiye amakhala Mulungu amene akuchita zimenezo pamenepo, osati ine. Ndi angati ati akhulupirire ngati Iye ati achite izo? Ine ndikuyembekezera pa Iye. Kwezani manja anu. Inu mukuti, “Ine ndikhulupirira izo. Inde, bwana. Ine ndikhulupirira izo, ndi mtima wanga wonse.” Chabwino.

206 Tsopano kwezani mitu yanu, pamene mukuyang'ana ndi kupemphera. Tsopano mofewa kwenikweni, nyimbo iyi. Apa pali limba lakale lomwe ine ndinalimva ilo koyamba.

Kungo khulupirira . . .

207 Yesu ankabwera kuchokera ku phiri, ophunzira Ake anali akuyesera kuti achize vuto la khunyu. Iwo sakanakhoza kuchita izo, ngakhale iwo anali nayo mphamvu. Iwo analibweretsa ilo kwa Yesu. Iye anati, "Ine ndingakhoze ngati inu mutakhulupirira, pakuti zinthu zonse ndi zotheka. Kungo khulupirira."

208 Aliyense molemekeza basi momwe inu mungakhalire. Mungoyang'ana mbali iyi, monga Petro ndi Yohane anati, "Uyang'ane pa ife." Osati kuyang'ana kwa iwo pofuna chinachake, koma kupereka chidwi. Anati, "Siliva ndi golide ine ndiribe."

209 Mulole Mulungu wa Kumwamba apereke izi. Mwaona, Mawu Ake ali pa nkhu, osati anga. Ine udindo wanga ndi kuwalalikira Iwo.

210 Izo ndizovuta, muno ndi mumzinda wanga womwe. Inu mukudziwa, Yesu anauzidwa, pamene Iye anapita ku mzinda Wake Womwe wa kwawo, Iye sanakhoze kuchita ntchito zambiri zamphamvu. Nonse a inu mukudziwa zimenezo. Ndipo Yesu anaima ndiye, anati, "Mneneri sadzakhala wopanda mphotho, kupatula ngati kuli ku mzinda wake womwe, pakati pa anthu Ake." Izo zikadali zabwinobe lero.

211 Koma pali ambiri pano omwe si a mzinda wakwathu.

212 Pa mapeto pomwe pa mzere apo, bwana, mukundiyang'ana ine, mwavala magalasi, ndikuganiza ndife alendo kwa wina ndi mzake. Mulungu akutidziwa awiri tonsefe. Koma inu mukudziwa kuti pali chinachake chachinsinsi chimene chikuchitika. Ngati mukanangokhoza kuwona chimene ine ndikuwona, pamwamba panu pomwe pali Kuwala kumeneko. Ngati Mulungu ati awulule kwa ine! Tsopano inu mukulumikizana naye Iye. Iye ayenera kugwiritsa ntchito liwu langa ndi maso anga. Koma inu mukusowa chinachake. Ine sindikukudziwani inu. Inu mukudziwa ine sindikudziwa kanthu za inu. Ngati uko nkulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu, bwana.

213 Koma inu mukuzindikira kuti inu muli ndi kumverera pa inu, kumverera kokoma kwenikweni, kodzichepetsa (Si kulondola uko?) pakali pano. Ameneyo ndi Mngelo wa Ambuye. Ali pamwamba panu pomwe. Ngati Mulungu ati awulule kwa ine lomwe liri vuto lanu, monga momwe Iye anachitira kupyolera mwa Mwana Wake, Ambuye Yesu; ndipo Iye anabwera kuti adzayeretse mtima wanga, kuti Iye adzakhoze kukhala moyo pano kuti adzayankhulenso ndi inu; kodi inu mungakhulupirire kuti ndi Wansembe Wamkulu

yemweyo amene inu mwamukhudza? Inu mukulumikizana ndi Chinachake. Ndi Iyeyo.

214 Vuto lanu liri mmapapo anu. Uko nkulondola. Kwezani mmwamba dzanja lanu. Izo ndi zoipa kwambiri mwakuti mukumalephera kugwira ntchito. Uko nkulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu. Ine sindikukudziwani inu.

215 Ndi angati akukhulupirira tsopano? Tayang'anani kuno. Inu mukuganiza kuti ine ndinapeka zimenezo. Mzimu ukadali pa munthuyo.

216 Inu mukukhulupirira Mulungu wa Kumwamba akukudziwani inu? Inu mukamutumikira Iye? Ine ndikuti, inu mukamutumikira Iye? ["Uko nkulondola."—Mkonzi]. Inde, bwana. Ndinu Mkhristu. Inu munabwera kuno ndi cholinga choti mudzachiritsidwe. Inu mukupita kwanu, wabwino. Dzina lanu ndi Bambo Raney. Uko nkulondola ndendende. Kwezani mmwamba dzanja lanu ngati izo ziri zoon. Inu mukhoza kubwerera kwanu. Inu mwachiritsidwa, bwana. Chikhulupiriro chanu chakuchizani inu. Mulungu akudalitseni inu.

217 Ine sindinayambe ndamuwonapo bamboyo mmoyo wanga, pano pali manja anga, mwinamwake nthawi yathu yoyamba. Ndi Mulungu. Tsopano khalani chete. Aliyense akhale mu pemphero. Inu mukudziwa kuti pali Chinachake pano chikuchita zimenezo.

218 Tsopano, Afarisi anati, "Iye ndi mdierekezi." Ndiye iwo analandira mphotho yake.

Filipo anati, "Ndi Mwana wa Mulungu." Iye analandira mphotho Yake.

Chirichonse chimene inu mukuganiza za Iwo, izo ziri kwa inu.

219 Inu amene mukulira pamenepo. Inu mumadziwa kuti Chinachake chinakukhudzani inu, sichoncho inu? Ngati izo nzoona, kwezani mmwamba dzanja lanu. Bambo yemwe akulira, wakhala pomwe pano, ndife alendo kwa wina ndi mzake. Ine sindikukudziwani inu. Koma Mulungu amakudziwani inu. Ngati Mulungu ati awulule kwa ine lomwe liri vuto lanu, kodi inu mukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Ngati inu mutero, gwedezani dzanja lanu mmbuyo ndi mtsogolo. Chabwino.

220 Inu mukuvutika ndi vuto la mmimba. Uko nkulondola. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu? Chabwino, inu mukutero. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akudziwa yemwe inu muli? Ngati Iye ati andiuze ine yemwe inu muli, kodi izo zikulimbikitsani inu? Ikani dzanja lanu mmwamba, ngati inu mukutero, gwedezani ilo mmbuyo ndi mtsogolo. Chabwino. Izo zikulimbikitsa inu? Bambo Fred Moore. Ndiko kulondola ndendende. Pitani kwanu, bambo, zilonda za mmimba zakusiyani inu. Izo zimayambitsa chikhalidwe cha manjenje

chimene chimachita zimenezo, koma Yesu Khristu wakuchizani inu pamene Iye anakukhudzani inu pamenepo.

²²¹ Dona wakhala pafupi ndi inu apo, oh, ine ndikudziwa yemwe iye ali. Ine ndikumudziwa mkazi ameneyo, amene dzina lake liri. . . Ine sindikulakwitsa. Ine ndikukhulupirira kuti ndi Akazi a Greene, si choncho? Ine sindingakhoze kukutchani inu, Mlono Greene, chifukwa ine ndikukudziwani inu. Koma, apa, dikirani miniti. Ayi, izo si za inu. Inu mukumupempherera winawake. Uko nkulondola. Ndipo munthu ameneyo ali mu dziko lalikulu kutali ndi kuno, kumene kumachita chisanu chambiri. Ndi ku Nebraska. Ndi dona amene ali ndi khansa, amene inu mukumupempherera. Ngati uko nkulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu. Munthuyo ali ndi khansa, yemwe inu mukumupempherera, mu Nebraska. Chabwino. Mulungu akudalitseni inu.

Khalani ndi chikhulupiriro! Mukhulupirire!

²²² Dona wakhala apoyo, akupukuta misonzi mmaso mwake, iye ndi mlendo kwa ine. Ine sindikumudziwa donayo. Ameneyo ndi mwamuna wake wakhala pafupi ndi iye; mwamuna wamkulu. Pokhala alendo!

²²³ Inu mukukhulupirira kuti Mulungu amamva pemphero? Inu mukukhulupirira kuti uwu ndi Mzimu wa Mulungu, dona? Inu muli ndi mthunzi wa imfa, sichoncho inu? Ndi khansa. Ndife alendo. Ngati uko nkulondola, gwedezani dzanja lanu mmbuyo. Uko nkulondola. Sindinayambe ndakuwonanipo inu, mmoyo wanga. Inu sindinu wochokera mu mzinda uno, ndinu wochokera kutsidya kwa mtsinje kwina wake. Uko nkulondola. Akazi a Sanders ndiro dzinalo. Uko nkulondola. Hilda ndi dzina loyamba. Ndiko kulondola ndendende. Imirirani pa mapazi anu, dona, ndipo mulandire machiritso anu kuchokera kwa Yesu Khristu. Mulungu akudalitseni inu. Mukuona?

²²⁴ Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Musati mukaikire. Ena, inu nonse mmizere iyi apa, mukhulupirire pa Ambuye Yesu ndipo inu mukhala bwino.

²²⁵ Tsopano, ndi Iyeyo. Kodi inu mukukhulupirira kuti ndi Iyeyo? Mwaona, ine sindikukudziwani inu. “Ngati inu mungakhulupirire!” Izo ziri kwa inu.

²²⁶ Inu mukuwoneka kuti mukupemphera, mwakhala pomwe apa, bwana. Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake? Inu mukukhulupirira kuti akanakhala Iye? Ndine mlendo kwa inu. Ndinu mlendo kwa ine. Ino ndi nthawi yathu yokumana. Koma Mulungu akutidziwa awiri tonsefe. Inu mukukhulupirira zimenezo? Zinthu zimenezo ndi zooni. Kwezani mmwamba dzanja lanu. Inu mukukhulupirira kuti inu mukupita kwanu opanda vuto lanu la nsana, Mulungu akuchizani inu? Inu mukutero? Kubwerera ku Ohio, Hamilton. Uko nkulondola. Dzina lanu ndinu Bambo Burkhart. Izo nzoona.

Yesu Khristu wakuchizani inu tsopano. Inu mukhoza kupita kwanu, mukakhala bwino. Amen. Winawakenso, khulupirirani.

227 Oh, kodi inu mukudziwa za Kukhalapo Kwake? Kodi inu mukuzindikira kuti Chinachake chiyenera kuchita zimenezo? Ndizo ndendende zomwe Baibulo linanena kuti Iye anachita poyamba, ndipo analonjeza... Iye anachita izo pamaso pa Myuda, pamaso pa Msamariya, ndipo analonjeza kuti adzachita izo pamaso pa Amitundu. Ora lake ndi lino. Osati Mulungu wina wa mbiriyakale; koma Mulungu Amene amasunga lonjezo Lake, amene akukhala moyo pakali pano; Ambuye Yesu, Mmodzi yemweyo Amene amachiritsa odwala, mwanjira yomweyo imene Iye anachitira izo, mwanjira yomweyo, ndipo analonjeza izo mmasiku otsiriza. Iyi ndi Khristimasi kenanso, Kuwala Kwake kotsogolera. “Kodi inu mukuyang’ana chiyani, M’bale Branham?” Ine ndikumuyang’ana Iye. Ndi dziko lina. Ndi dera lina, ngati inu mukufuna kulitchula ilo limenelo. Ilo liri mu dziko la mzimu.

228 Ine ndikumuwona munthu, wa mtima-wojintcha kwenikweni, koma ine ndikumudziwa iye. M’bale Funk, ine sindimadziwa izo mpaka pakali pano. Inu muli mu vuto. Mthunzi wakuda weniweni pa amayi anu. Ndipo inu mukudziwa ine sindikudziwa zimenezo; ine ndimangobwera muno. Koma amayi anu anakhalapo ndi opareshoni, ali ndi chotupa, khansa. Inu mukudandaula za iye, ndipo inu mukupemphera. Mulungu amene anawabwezeretsa abambo anu kuti aziganiza bwino, anawabwezera iwo thanzi lawo, akhoza kuwabwezeretsa amayi anu. Musati muwope. “Ngati inu mungakhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira.”

229 Ndi Uyo apo, pa munthu wina, koma ine ndikumudziwa iye. Koma iye akumupempherera winawake. Akazi a Arganbright, ngati inu muti mukhulupirire izo, khansa imeneyo ichiritsidwa. Ndi kwa munthu winawake. Inu mukhulupirire.

230 Nanga bwanji inu? Inu mukukhulupirira, dona, ine kukhala mneneri Wake, wantchito Wake? Inu mukuvutika ndi chinthu chomwecho chimene mkaziyo anali, vuto la magari. Kulondola. Inu sindinu wochokera mu mzinda uno. Ndinu wochokera ku Ohio, nanunso. Ndipo inu mwangochiritsidwa kumene mu umodzi wa misonkhano yanga, ku chinachake, inueni. Inu munali ndi khansa. Inu munali ndi mthunzi wa imfa, ndipo iwo wapita tsopano. Uko nkulondola. Kuti inu mukhoze kudziwa kuti ine ndine wantchito Wake, nkhani ya magari ndi yochokera mu m’badwo wanu. Koma inunso muli ndi kupweteka kwa mafupa, kapena monga nyamakazi, iyo ili, pamene inu mukudzuka. Inu mumauma mmawa. Inu muli ndi vuto ndi mmero wanu, nanunso. Inu mukundikhulupirira ine kukhala wantchito Wake?

231 Inu muli naye winawake pa mtima wanu, inu

mukumupempherera. Ndi mpongozi wanu wamkazi. Iye ali ndi mitsempha yotupa. Iye ndi mayi wa gulu lalikulu la ana. Sichoncho iye? Uko nkulondola ndendende. Dzina lanu ndi Mayi Alice Thompson. Nkulondola ndendende. Bwererani, mulandire chimene inu mwachipemphacho. Chotero *iye* adzachiritsidwa, chifukwa inu mwakhulupirira pa Ambuye Yesu. Tsopano ngati ife tiri alendo kwa wina ndi mzake, gwedezani, gwedezani dzanja lanu mmbuyo ndi mtsogolo, monga *chonchi*. Ine sindikukudziwani inu, sindikudziwa kanthu za inu.

²³² Ine ndikutsutsa chikhulupiro chanu. Ine ndikutsutsa munthu aliyense muno, mu Dzina la Yesu Khristu, kuti akhulupirire mu Kukhalapo Kwake. Ine sindikusamala chimene chakuvutani inu, ngati inu muti mukhulupirire Izo.

²³³ Kumbukirani, ichi ndi chinthu chotsiriza chimene Iye ati adzachite kusanafike Kudza Kwake. Inu mukukumbukira zimene Iye ananena? “Monga izo zinali mmasiku a Sodomu ndi mu Gomorrah, chomwechonso izo zidzakhala mu Kudza kwa Mwana wa munthu.” Uthenga unali chiyani?

²³⁴ Panali Angelo atatu anapita kumeneko. Awiri a iwo, Billy Graham ndi Jack Shuler anapita uko ku Sodomu, ndipo anangokalalikira uthenga wa chiwombolo cha Uthenga, kwa anthu. Koma Mngelo mmodzi anatsalira mmbuyo ndi osankhidwa, Abrahamu ndi gulu lake.

²³⁵ Ndipo Mngeloyo anali atatembenuzira nsana Wake ku hema. Ndipo Sarah anaseka, mkati mwa hema. Ndipo Mngelo anati, “Nchifukwa chiyani Sarah waseka?” Kodi Iye anadziwa bwanji kuti iye anaseka, mu hema kumbuyo kwa Iye? Uwo unali uthenga wotsiriza umene Sodomu anali nawo chiwonongeko chisanachitike.

²³⁶ Ndipo apa pali zizindikiro zotsiriza zimene Mulungu ati adzasonyeze chiwonongeko chisanachitike. Landirani izo, khulupirirani izo, ndipo mupulumutsidwe.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu kamphindi chabe.

²³⁷ Kodi inu mukudziwa za Kukhalapo Kwake? Kodi inu mukumufuna Iye tsopano, Iye atatha...inu...Ine ndalalikira Uthenga kwa inu, ndipo inu mwamva Uthenga Wake. Ndiye inu mwamuwona Iye akubwera paamenepo ndipo kuyankhula, Iyemwini. Munthu akhoza kunena chirichonse; koma kupatula ngati Mulungu atayankhula ndi kutsimikizira izo, izo sizabwino. Koma pamene Iye abwera, Mulungu, ndi kudzapanga Uthenga kukhala weniweni, ndi kudzakhalanso moyo, ndiye ndi Mulungu. Kodi inu mukufuna kumulandira Iye tsopano mu kugonjera kwathunthu kwa moyo wanu? Kodi inu mungakweze manja anu mphindi chabe, ndikuti, “Ine ndikukweza manja anga. Ine tsopano ndikupereka zanga zonse, zanga zonse kwa Iye.” Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu.

²³⁸ Onse amene ali osowa pemphero, la machiritso, ine ndikukhulupirira kuti aliyense wa inu achiritsidwa. Tiyeni tiwapempherere odwala.

²³⁹ Ambuye, kuti pasakhale wina wosiyidwa kunja, kuti onse akhoze kulandira! Ife tikuzindikira, Ambuye, pamene ine ndiri... ndayima pano wofooka ndi wonjenjemera, Inu muli pano. Izo ndi zoposa mthunzi uliwonse wa kukaikira. Anthu amakanthidwa ndi kuwopsya kwa Kukhalapo Koyera kwa Mulungu, Khrisimasi ina, Kuwala kwauzimu komweko kukuwala. Iko kwawatsogolera ambiri kuchokera kumayendedwe osiyanasiyana. Iwo amva Mawu Anu akuwerengedwa, ndipo akulalikidwa, ndipo tsopano akuwoneni Inu mukubwera ndipo mudzatsimikizire Mawu.

²⁴⁰ Baibulo linati, “Ophunzira anabwerera, ndipo anakalalikira Mawu konsekonse, Ambuye akugwira nawo ntchito, akutsimikizira Mawu ndi zizindikiro zikuwatsatira,” zinthu zotsiriza zimene zinalembedwa mu Malemba, kunja kwa Vumbulutso. Tsopano ife tikuziwona izo kachiwiri. Izo ziri pafupi ndi Kudza, Ambuye. Tichitireni chifundo. Achizeni odwala onse amene ali pano mmawa uno. Mzimu Wanu ndi woona. Ndi wamphamvu, ndipo Iwo uli pano.

²⁴¹ Ndipo alipo ambiri pano, Ambuye, amene ali anthu a pa kachisi, amene amabwera kuno. Inu mwakhala wachifundo kwa iwo, kuwaitana iwo.

²⁴² Ndipo, komabe, Ambuye, Iwo uli pa omvetsera onse, pakali pano. Ulemelero waukulu wa Shekinah, Mphamvu yaikulu ya Khristu wowukitsidwa, Utawaleza wa mitundu yambiri, Alfa ndi Omega, Chiyambi ndi Mapeto, Nyenyezi ya Mmawa, Rozi la Sharoni, liri pano. Achizeni, Ambuye. Ife tikuwalengeza iwo kuti ali bwino, kupyolera mu chisomo Chanu. Apatseni iwo chikhulupiriro kuti akhulupirire izo, Ambuye, ndipo mulandire izo pakali pano, kwa ulemelero wa Mulungu. Mulole munthu wodwala aliyense achiritsidwe.

²⁴³ Ndipo munthu aliyense amene walakwitsa, amakhala moyo-... wolakwika kwa mkaze, mulole iwo akhululukidwe. Munthu aliyense amene amasuta kapena kumwa, mulole iwo akhululukidwe. Mulole machimo awo akhale pansa pa Magazi, ndi Mulungu wopezeka ponseponse Yemwe ali pano tsopano; mwinamwake chapafupi kwambiri chimene iwo anayamba akhalapo kwa Iye, mmoyo wawo wonse. Perekani tsopano kuti izi zilandiridwe.

²⁴⁴ Timvereni ife, Ambuye, O Mulungu, Mfumu yathu yaikulu, pamene ife tikuitanira pa Dzina Lanu, mu nyengo ya chisangalalo iyi; osati Santa Claus; koma Yesu amene anawuka kwa akufa, ndipo ali moyo, kudzisonyeza Yekha pakati pa anthu Ake. O Ambuye, Inu ndinu Mulungu, ndipo Mulungu yekhayo, ndipo palibe wina koma Inu. Ndipo ife

tikukuthokozani Inu kuti ife tiri nawo mwayi wa kukhala mu Kukhalapo Kwake, mmalo aang'ono awa, odzichepetsa. Iye anadzichepetsa Yekha ndipo anabwera pakati pathu. Ndife okondwa kwambiri chifukwa cha izi! Lodala likhale Dzina Lake loyera! Ife tikumupatsa Iye matamando, kuyambira mmawa mpaka usiku, ndi kudutsa nyengo zonse za usiku, mitima yathu ikuimba nyimbo ndi matamando a Yehova. Mathokozo akhale kwa Iye, kwanthawi zanthawi!

²⁴⁵ Atengereni awa, ana Anu, Ambuye, pansi pa mapiko Anu, muwaphimbe iwo monga nkhuku imachitira anapiye ake. Atsogolereni iwo kukalowa mu Moyo wakuya, ndi ku moyo wosangalala, ndi ku moyo wodzadza kwambiri, apatseni iwo ubatizo wa Mzimu Woyera. Isintheni miyoyo yawo, Ambuye, akakhale zolengedwa zatsopano mwa Khristu, kuti Inu mukakhoze kukhala moyo ndi kumakhala mwa iwo, ndi kumagwira ntchito kupyolera mwa iwo, monga ophunzira Anu. Perekani izi, Ambuye. Pakuti, ife tikukhulupirira kuti posachedwapa mlengalenga mudzasweka ndipo Ambuye wathu adzabwera, ndipo ife tidzamuwona Iye Amene ife timamukonda. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha izi, kupyolera mwa Yesu Ambuye wathu.

²⁴⁶ Tsopano ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ine ndikutembenezira msonkhano kwa abusa. 

58-1221M Ali Kuti Iye, Mfumu Ya Ayuda?
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org